


CHIZINDIKIRITSO

 Mukhoza kukhala pansi. Zikomo kwambiri, m'bale, M'bale Shores. Ndi a... Ine ndithudi ndikuchiwona ichi ngati chamwayi waukulu kukhala pano usikuuno, mu... First Assembly of God iyi, kachiwiri, kudzayanjana pozungulira Mawu a Mulungu, ndi inu anthu abwino, kudzakhala ndi M'bale wathu wofunika Shores kenanso, ndi—ndi abale onse amene takumana nawo kudutsa m'sabatayi. Ndipo ife takhala nayo kwenikweni nthawi yabwino kwambiri, masabata awiri apitawa.

² Ine sindikudziwa monga momwe ndakhalira, mu zaka, ngati ndinakhlapo ndi nthawi yabwino kuposa imene ndinakhala nayo sabata ino, ya kuyanjana ndi abale kuzungulira mu Chigwa cha Maricopa ichi, njira yonse kuchokera ku Mesa, kutsika, ndipo mpaka kukafika ku Tucson, kumene kuli ku Yerusalemu, ndithudi, pa phiri. Ndipo ndife okondwa kudzacheza ndi abale athu kuno mu Yeriko, mwaona, kumusi kuno mu... kumusi pansi pa phiri. Ine ndimangodabwa momwe izo zikanati ziyendere.

³ Ndipo chotero pamene ine ndinali kuno, zaka zambiri zapitazo, umenewo nthawizonse unali mkangano pakati pa Tucson ndi Phoenix. Chotero, ine ndimangoganizira za zimenezo tsiku lina, inu mukudziwa. Iwo ankandinena ine chifukwa chokondera Tucson. Ndipo kotero ine ndinaganiza za, chabwino, iye ali pa phiri, ndipo Yeriko ali mu chigwa, inu mukudziwa. Kotero ine ndinaganiza kuti izo zikanakhala zabwino basi. Chabwino, ife tinawapeza Bambo pakatipo ndiye, wina akubwera kumusi. Ife tikufuna tichite naye iye.

⁴ Tsopano, iyo yakhala ili nthawi yabwino, monga ndikubwerezera, ndipo ife mwamtheradi tasangalala kwambiri ifeeni.

⁵ Tsopano, ife ndi oya-...tikudikirira ndi chiyembekezo chachikulu ku msonkhano wawukulu umene ukubwerawu kuyambira mawa usiku. Ife tikuyembekezera nthawi yopambana. Ndipo mu ichi ine ndayesetsa kuyika, mwanjira yanga yodzichepetsa yochitira izo, maziko, kukhala ngati kupeza kukondoweza pakati pa anthu, kwa chitsitsimutso chimene chikubwerachi. Ndipo tsopano ife tiri ndi oyankhula odabwitsa amene akubwera, mu chitsitsimutso ichi chimene chiri pafupi tsopano. M'bale Velmer Gardner, ndi—ndi m'bale wina wa Methodisti amene akuyenera kudzakhala woyankhula wapamwamba, ndipo kenako, kwa kumalizitsa kwakukulu kotsiriza kumeneko kwa izo zonse, adzakhala M'bale wathu wofunika Oral Roberts, Lolemba likubwerali usiku. Ndipo ine

ndikudalira kuti Mulungu adzawapatsa abalewo mauthenga oterowo amene ati adzabweretse Phoenix ku mawondo ake, akunjjemera, mu kuwopa Mulungu.

⁶ Ndipo ife tinayesetsa zamphamvu, sabata ino, kuti—kuti tiyike maziko a zimenezo, a kuwonekera kwa posachedwapa kwa Mwana wa Mulungu. Ndipo ine ndikukhulupirira, ndipo ndakhala ndikuphunzitsa, kuti zonse pamodzi nzotheka kuti Iye akhoza kubwera mu m’badwo uno tsopano, ngakhale usiku uno. Ife sitikudziwa basi kuti izo zidzachitika liti, koma ife tikufuna kuti tikhale okonzeka kwambiri kuti, pamene izo zikubwera, ife tidzapite ndi Iye mu Mkwatulo.

⁷ Iyo yakhala ili nthawi yopambana. Ine ndakhala ndikulalikirira Mauthenga amphamvu awa okhudza Kudza Kwake, ndi kuyesetsa kuyika a—zothekera, ndi ora limene ife tikukhalamo tsopano, ndi momwe kuti chirichonse, mwa kuganiza kwanga, lingaliro langa lodzichepetsa, chiri mu chikhaliidwe basi cha Kudza kwa Ambuye, Mkwatulo, chinthu chotsatira. Ndipo zonse zimene zikusowekera, zikhoza kuchitika mu ora limodzi.

⁸ Ine ndikukhulupirira, ambiri, sindikudziwa basi kuti ndi angati, koma ena mwa maulosi opambana okhudza kukwaniritsidwa kwa kudza kwa Mesiya ndi chimene Iye akanati adzachite, zinakwaniritsidwa mu maora seveni otsiriza pa mtanda. “Momwe iwo anapyozera mbali Yanga, ndi Yanga . . . palibe fupa limene linathyoka.” Ndipo—ndipo Iye anafuula, “Mulungu wanga, ndi chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?” Ndi mauneneri aakulu, iwo anangochitika, wani, thuu, firii, foro, basi monga choncho, mu ora limodzi basi kapena awiri, kutalikana kwake.

⁹ Tsopano, izo zikhoza kuchitika mwanjira yomweyo pa kubweranso Kwake. Ndipo ife tikuyenera kukhala atcheru, tikudikirira.

¹⁰ Usiku wathawu ndimaganiza kuti tinali ndi nthawi yabwino kumusi ku—ku Assembly of God kummwera kwa kuno. Ine ndikukhulupirira kuti ndi Southside, mwinamwake, iko kumatchedwa, Southside Assembly. Ndinakumana ndi m’bale wabwino amene sindinakumanepo naye mu ulendowa, momwe ine ndikukumbukirira, koma m’bale wofunika ndi gulu labwino la anthu.

¹¹ Ndipo ife tinayankhula pa, kumeneko usiku wathawu, Uthenga wa . . . wa kukhala ndi Iye ngati kasupe, malo, kumukumbukira Iye, zonse zomwe Iye anachita, pamene ife tibwera pamodzi, titakhala pozungulira mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu. Ndi kukumbukira zinthu zimene Iye anazichita, ndi zinthu zimene Iye analonjeza kuti adzazichita, momwe Iye analonjezera kuti Iye akanadzakomana ndi ife. “Kulikonse kumene awiri kapena atatu asonkhana

mu Dzina Lake, kuti kumeneko Iye akanadzakhala pakati pathu.” Ndiye, ine ndinaganiza kuti kuchita kwayekha kwa Mulungu kunawonetseredwa modabwitsa kwambiri pamene Iye anabwera pansu pomwe pakati pathu, ndipo anadzitsimikizira Iyemwini, kuti Iye anali pamenepo ndi ife kachiwiri. Izo zimangopangitsa izo kuti zikhale zotsimikizika kwambiri, kuti tayandikira mapeto. Ndipo zinthu zimenezo zimene Iye analonjeza kuti akanadzazichita, pa mapeto pomwe, ndipo ife tikuziwona izo zikuyang’anizana ndi ife tsopano.

¹² Ine ndikupenekera, mwinamwake, kuti anthu ambiri pano ndi—ndi anthu opulumutsidwa. Ndipo ife ndi amene tikupemphera ndi kuyikapo khama lathu tsopano chifukwa cha msonkhano ukubwerawu. Ndipo ife tikuyenera kumenyera ndi zonse zomwe ziri mwa ife, ndi kuchita chirichonse chimene ife tingathe. Tiwonetsetse kuti tiyankhule ndi wochimwa aliyense pa nthawi ya msonkhano wawukulu umenewu. Mufikireni wamalonda aliyense, ndi munthu wosapulumutsidwa aliyense, ndi iwo opanda Khristu, opanda Mzimu Woyera. Ife tikufuna kuti tiwafikire iwo ndi Uthenga, ndi mafikidwe abwino, mafikidwe okhazikika a Uthenga kwa anthu.

¹³ Miyoyo yathu ikhale ya mchere, kuti ena azitha kuwona momwe ife tikuchitira ndi kukhalira, kuti iwo afune kukhala mwanjira imeneyo, nawonso. Inu mukudziwa Yesu anati, “Inu ndi mchere wa dziko lapansi.” Koma ngati mcherewo wataya umboni wake, kwake—kukoma kwake, mphamvu yake yokoka, ndiye iwo sungathenso kuchiza kapena kupulumutsa. Mchere umakometsa pamene ufikirapo, ndipo ife tizikhala—tizikhala zofikirapo za Mulungu. Ifeyo ndife zofikirapo Zake, monga M’bale Roberts nthawi zambiri amakamba za kuyika dzanja lake pa walesi kapena chinachake kukhala malo olumikizira.

¹⁴ Tsopano, inu mukhoza kundimva ine ndikuyankhula mwachirendo pang’ono usikuuno, koma mausiku atatu kapena anayi apitawa ndimayenera kukweza mawu anga pamwamba. Ine—ine. . . Enawo asasa. Koteru, ndikuyankhulira mmwamba, mochuluka kuchokera pamwamba pa kamwa yanga. Sikuti ndi zodzipangitsa, koma ndikuyenera kuchita zimenezo, kupewa kuti gawo lapansi lisapweteke. Inu mukudziwa, Mulungu anakhala ngati anatipanga ife mwanjira, yakuti, ngati gawo limodzi lifooka, ife tikhoza kugwiritsa ntchito linalo. Winawake—winawake. . . Inu mukudziwa, losungira.

¹⁵ Ndipo winawake anandifunsa ine, wina, nthawi ina, anati, “Inu mumakhoza bwanji kuyenda mwamphamvu chomwecho kudutsa mmapiri ndi zina zotero?”

¹⁶ Ine ndinati, “Chabwino, ine ndinaphunzira zimenezo, kachitidwe kakang’ono, zaka zambiri zapitazo, kuchokera kwa Amwenye.” Mukuona? Iwe ukhoza kuyenda ndi mawondo ako, osagwiritsa ntchito kwambiri, chiuno chako, ndi kusiya

chiuno chako kuti chipume. Kenako nkudzayenda ndi chiuno chako, ndi kudzasesereka, ndi kulola mawondo ako apume, inu mwaona. Kotero umangopuma ndi kuyenda, kupuma ndi kuyenda, kupuma ndi kuyenda.

¹⁷ Umo ndi momwe umalalikirira, ndi la mmwamba kenako la mmusi, mmwamba ndi mmusi. Kulola limodzi lipume, linalo.

¹⁸ Oh, Mulungu anapanga chinthu chodabwitsa pamene Iye anamupanga munthu! Inu mukudziwa chifukwa chake? Munali mu chifaniziro Chake mmene Iye anamupangira munthu. Ndipo kotero nchiyani chinanso chimene chingakhale chodabwitsa kwambiri kuposa Mulungu?

¹⁹ Ine ndakhala ndikulalikira kwambiri pa—pa Kudza kwa Khristu mu m'badwo uno, ine ndimaganiza kuti mwinamwake chingakhale chinthu chabwino usikuuno ntakhala ngati ndakhazikika pa zina mwa zinthu izi zimene ine ndakhala ndikuzikamba, ndi kubweretsa a—kuyipa kwa chikhaliidwe cha tsiku lino, kuchibweretsa pamaso pathu, mwa Uthenga, ndikuwona momwe ife tiriri, ifeeni, momwe takhalira mu ora lino. Kodi ife tingadziwe bwanji? Uwu ukhoza kukhala msonkhano waukulu wotsiriza umene Amuna Amalonda awa ati adzakhale nawo konse. Inu mukudziwa, uwu ukhoza kukhala usiku wotsiriza umene First Assembly of God ndi mipingo ina yonse kudutsa mdziko lonse idzatsegulidwe. Mawa, zikhoza kudzachitika, iyo yonse yatsekedwa. Ife sitikudziwa. Aka kakhoza kukhala kotsiriza kuti Baibulo liweringedwe kwa omvetsera. Chotero, tiyeni ife tingokhala ngati tidzifufuze usikuuno ndi kuwona pamene ife tiri, chifukwa cha kuipa kwake, kwa kanthawi pang'ono.

²⁰ Ndipo kenako ife tipita, tiyesetsa kuti timalize molawirira, kuti ife tikhoze kuwatulutsa anthuwo ndipo osakugwirani inu. Ine ndinapanga ndemanga yaying'ono yamwano sabata ino, kuti ine—ine ndimakusungani inu motalika mu nthawi ya usiku, ngati nditangodziwa kuphonya ntchito ya tsiku limodzi, zimenezo sizingakupwetekeni inu. Koma ine ndinati, “Loweruka usiku tsopano, sindingakusungeni inu motalika nkomwe, chifukwa inu simungakhoze kuphonya Sande sukulu. Inu mukuyenera kukakhala kumeneko pa malo anu antchito.” Kotero, tsopano, ine sindikusungani inu motalika usikuuno, chifukwa ine ndithudi ndikukufunani inu kumeneko mawa usiku. Icho ndi chimene ife takhala tikuyendetsa, nthawi yopambana iyi.

²¹ Ndipo tsopano muwapempherere abale onse amenewo amene ati adzayankhule. Mupemphere kuti Mulungu adzawadzoze atumiki Ake. Ndipo usiku wathawu, ndi M'bale Oral; iye wasankhidwa kuti adzamalizitse kumeneko zonse za zimenezo. Ndikuganiza za nthawi yotsirizira ija, ngati kuti linali tsiku lotsirizira la phwando pamene Yesu anaimirira

ndi kufuula pa kachisi. Oh, mulole ife timve izo kachiwiri. Mulungu afuulire kwa ife, ndi kutiyitanira ife ku mbali Yake, kusonkhanitsa mu Mpingo, owomboledwa Ake, Mkwatibwi Wake amene Iye mwachisomo anamugula ndi Magazi Ake Omwe. Ndipo ife tikupempherera mathero amenewo.

²² Tsopano ife tiyang'ana kwa Ambuye pakali pano mu pemphero ife tisanayandikire Mawu Ake. Chifukwa, inu mukudziwa, Mawu alibe kutanthauzira kwamseri, kotero ine ndimangokonda kuti Mlembiyo awawulule Iwo; ndi kuchokako kwa Iwo, inu mukudziwa, basi kuti ife tikhoze—ife tikhoze kukhulupirira kuti Iye akuchita zimenezo. Kotero tiyeni ife tiweramitse mitu yathu pakali pano. Ndipo—ndipo pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, tiyeni tiweramitsenso mitima yathu, tingoweramitsira mitima yathu kwa Mulungu.

²³ Tsopano ndi mitu yathu ndi mitima yoweramitsidwa, kodi pali chopempha mu mtima mwanu usikuuno, mzika imzanga ya Ufumu, m'bale wanga mwendamnjira? Inu amene mukuchitira umwendamnjira kuno ku Phoenix ndi malo ena, amene tasonkhana mu tchalitchi chaching'ono chokondedwa ichi usikuuno kuti tidzamupembedze Iye, kodi pali chopempha chimene mungafune kuti Mulungu achidziwe? Chigwireni icho mmalingaliro anu, ndipo mungokweza dzanja lanu, ndi kunena, “Ambuye, mulole ndikhale ine tsopano usikuuno. Ine—ine ndiri ndi a—chosowa chosimidwa.” Mulole Iye. . . Ine ndikudziwa Iye achiwona icho. Iye achimva icho. Iye ayankha icho.

²⁴ Atate athu Akumwamba, ife tikukuyandikirani Inu mwa chikhulupiriro tsopano. Ife tikudzilumikiza tokha pamodzi, kuyika mapemphero athu ngati munthu mmodzi. Mwa chikhulupiriro ife tikuchoka pano, pa 11th ndi Garfield, ndipo ife tikukwera mmwamba mwa chikhulupiriro, kudutsa mwezi ndi nyenyezi, mpaka ku Milky White Way, kumapitirira ndi kudutsa zochitika za dziko lino, mpaka mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ndipo pamenepo pa Guwa pamene pali Nsembe, ndipo Akerubi ndi Aserafi akuwulukira pamwamba pa Guwa la Mulungu, akufuula, “Woyera!” Oh, ndi malo otani kuyimapo! Koma ndi Mawu olembedwa awa, mwa Mwana wa Mulungu, kuti, “Ngati ife tiwapempha Atate chirichonse mu Dzina Lake, Iye adzapereka icho kwa ife.” Ndipo pamenepo Iye wakhala ali ndi zovala Zake za Magazi. Mtengo walipiridwa, kuti ife, osayenerafe, tikhoze kumufikira Iye, monga ana aamuna ndi aakazi, ife titatha kumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wathu.

²⁵ Ndipo ife tikupemphera, Atate Akumwamba, usikuuno, choyamba, kuti mukhululukire kusaeruzika kwathu, ndi zonse zomwe ife tazichita ndi kuzinena, zimene sizinali zoyenera pamaso Panu. Ndipo, Mulungu, ife tikudziwa kuti izo ndi zinthu zosawerengeka zomwe ife tazichita. Tichitireni ife chifundo, Mulungu, pakuti ife sitikungoyankhula zinthu izi kuti timvedwe,

koma ife ti—tikuyankhula zinthu izi mu—mu chikondi, ndi mwa ulemu, ndi mwa chikhulupiriro kuti Mulungu atimve ife ndi kuyankha mapemphero athu kwa ena ndi ifeeni. Inu mukudziwa chimene chinali kumbuyo kwa dzanja lililonse, cholinga komanso chifukwa chake.

²⁶ Ambuye, mutambasule mapiko Anu aakulu oyera, monga izo zinali, usikuuno. Ndipo mulole Kukhalapo Kwanu kolemekezeka kumvereredwe pakati pathu, usikuuno, kuti ife tiwope. Mulungu, ife tikufuna kuti tingodziwa malo omwe ife tayimapo tsopano. Ife tikufufuza, tikupanga kafukufuku wa miyoyo yathu. Izo zikhoza kukhala basi Mkwatulo usanachitike, kuyitanira kutali.

²⁷ Ndipo tikuyembekezera msonkhano ukubwerawu ku Ramada mawa usiku, ndipo ife tikufuna kuti tifufuze miyoyo yathu yomwe usikuuno ndi kuwona pamene ife tikuperewera, kuchitira kuti tidzakhale zida m’dzanja Lanu, dongo lowumbidwa ndi lopangidwa ndi Mulungu wa Kumwamba, kuti tidzakhoze kuyembekezera mu chochitika chachikulu ichi chimene chiti chidzachitike, kuti sitikuchita pa chifukwa china koma chifukwa cha Ufumu ndi ulemelero wa Mulungu. Mudalitse kuyesetsa kwathu kofooka kwa sabatayi, Ambuye, kuyesetsa kuti tikondoweze, pakati pa anthu, kuzindikira kwa ora limene ife tikukhalamo.

²⁸ Muyankhule nafe usikuuno, kupyolera mu kuwerenga kwa Mawu, ndipo Inu mutenge phunzirolo ndi—ndi kuwulula nkhaniyo mwanjira imene Mzimu Woyera ungafunire kuti ife tidziwire zimenezo. Ndipo matamando onse adzakhala Anu. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

²⁹ Monga momwe anthu ambiri amakondera kumalemba maphunziro, ndi kuganizira za nthawi zomwe iwo angafune kubwerera kwa izo. Ndipo nthawi zambiri, atumiki, monga ine ndimachitira, inemwini, ife—ife timalemba phunziro nthawizina, kuti tidzalozere kwa izo. Mtumiki wina anayankhula pa zimenezo, ndipo ife. . . Lingaliro lina laling’ono linagwira maganizo athu. Ndipo ife timakonda kubwereranso kwa izo, nthawizina, kudzanena kuti, “Chabwino, ndizo. . . Ine ndinawona chinachake pamene iwo ankanena izo.” Izo zonse nzabwino.

³⁰ Tsopano, ife tikufuna kuti tiwerenge usikuuno, mu Baibulo, kuchokera mu bukhu la kalata ya Afilipi, Paulo akuwalemba Afilipi, mu mutu wa 2, 5 mpaka 8. Tikufuna kuti tiwerenge izi kuti tipeze mutu, pamene inu mukuwerenga nafe, kapena tipatseni ife tcheru chanu chosagawanika pamene tikuyesera kuti tiwerenge Ilo.

³¹ Tsopano, pamene inu mukutembenezira ku malo a mu Lemba, ine ndikufuna kunena kuti izo zaperekedwa kwa ine, m’bale wanu, mwayi wokayankhula Lamlungu likubwerali

masana ku msonkhano waukuluwo. Icho chinali cholinga changa kuti ndidzakhale ndiri kumeneko tsopano sabata yonseyo, ndi kukakhala uko penapake mwa omvetsera, kapena penapake, kumamvetsera ndi kumadzazitsa ndi kumadyetsera solo yanga yomwe pa Mawu a Mulungu, mmene abale athu azidzabweretsera izo, ndi maumboni a amuna amalonda. Ndipo ndikuyembekeza kukakuwonani inu nonse kumeneko. Msonkhanowo udzakhhalapo masana, kotero matchalitchi adzakhala atatekedwa, kuzungulira konseko, inu—inu mudzakhala olandiridwa kwambiri mukadzabwera. Ife tikukuyembekezerani inu, umenewo ndi msonkhano wina uliwonsewo.

³² Tsopano mu Afilipi 2:5, tikuwerenga.

Mulole malingaliro awa akhale mwa inu, amene analinso mwa Khristu Yesu:

Amene, pokhala m'mawonekedwe a Mulungu, sanachiyese cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu:

Koma anadzipanga yekha wopanda mbiri, ndipo anadzitengera pa iye mawonekedwe a wantchito, ndipo anapangidwa mu chifaniziro cha anthu:

Ndipo popezedwa mmawonekedwe ngati a munthu, iye anadzichepetsa yekha, ndipo anadzakhala womvera ku imfa, ngakhale imfa ya pa mtanda.

³³ Ambuye awonjezere madalitso Ake ku kuwerenga kwa Mawu Ake. Ndikufuna kuti nditenge, kwa maminiti ochepa a nthawi yanu, pa chimene ine ndingachitchule, kapena ngati kunena, mutu wotchedwa: *Chizindikiritso*. Kuzindikiritsa, kuzindikiritsidwa mu chifaniziro cha anthu a mu Baibulo! Kuzindikiritsidwa mofanana ndi anthu a mu Baibulo! Ndipo usikuuno, monga ine ndinaganizira, poyandikira ku izi, ife titatha sabata ino kuyankhula za Kudza Kwake, ndi momwe Mpingo ukuyenera kudzikonzekeretsera Wokha.

³⁴ Lero pamene ndinakhala mchipinda, ndinali ndi chinachake mmalingaliro mwanga chimene ndimafuna kuti ndiyankhulepo usikuuno, “Nsembe yapamwamba.” Koma, zimawoneka, Mzimu Woyera umawoneka ngati umandisuntha ine chammwali kuchoka ku chimenecho, kupita mu mpita wina wa kuganiza. Atumiki onse akudziwa chimene icho chiri, iwe—iwe umaganiza kuti uli ndi chinachake chomwe ukufuna kunena, ndipo kenako, mwadzidzidzi, iwe umamverera kuti ukuyenera kunena chinachakenso, mwinamwake chosiyana. Mwinamwake ndi cha munthu mmodzi. Ine sindikudziwa. Koma, ndine wamkulu mokwanira mwa Khristu, kudziwa kutsatira kutsogolera kwa Mzimu. Chimene Mzimu akunena kuti uchite, chita chimenecho.

³⁵ Ine ndikutsimikiza usikuuno kuti ife tikuyenera kudzipeza tokha penapake mu khalidwe linalake la m’Baibulo, kotero kuti

tidziwe zotsatira za khalidwe limenelo ndi kudziwa chimene chotsatira chathu chidzakhale.

³⁶ Zikundikumbutsa za nkhani yaying'ono imene ndinaimvapo nthawi ina, ya a—dona, anali atamubweretsa mwana wake wamng'ono kuchokera—kuchokera kumudzi kwinakwake, kumene iwo ankakhala, kubwera mu mzinda, ku—kudzawachezera agogo ake. Ndipo mnyamata wamng'onoyo, ankakhala kumbuyo. . .

³⁷ Ku dera langa la dziko, ku Kentucky, *kumudzi* kumatanthauza m'nyumba ya zipika kwinakwake, yokhala ndi denga la mabolodi ena akale pa iyo. Ndipo kotero kalilole wathu, kunyumba, anali chidutswa cha galasi litakhomeredwa pa mtengo, kumene, kunjako, komwe kunali ka benchi kakang'ono kosambirapo katamangidwa pa mtengowo, pafupi ndi mjigo, kumene bambo ankapopa madzi ndi kusamba mmanja, ndi chidutswa cha galasi chiri pamenepo. Ndipo ine ndawawonapo Amayi atayima kunja uko ndi kumapesa tsitsi lawo, chifukwa munalibe galasi mnyumbamo.

³⁸ Mwana uyu ayenera kuti analeredwa mnyumba yoteroyo. Ndipo pamene iye anabwera kudzawachezera agogo ake aakazi, iwo anali ndi—chitseko chimene, kuseri kwake, kunali galasi. Ndipo mnyamata wamng'onoyo anali ngati wosungulumwa. Ndipo ankayang'ana paliponse m'nyumbamo. Ndipo patapita kanthawi, iye anasuzumira pa chitseko. Ndipo icho chinali chotsekedwa, chilowereni iwo. Ndipo—ndipo pa galasi kumbali yake, iye anawona mnyamata wamng'ono. Ndipo anayamba kumapita kwa mnyamata wamng'onoyo, kuti apange ubwenzi ndi iye. Ndipo pamene iye anayamba kuyang'ana pa galasi ili, iye anayandikira pafupi. Ndipo iye anatembenuka, iye anati, “Bwanji, amayi, uyo ndi ineyo.”

³⁹ Ndipo izo ndi zimene ife tikufuna kuti tiyang'anepo usikuuno. Ine ndikufuna kuti ndiyang'ane pa ine, ndipo ine ndikufuna kuti inu mudziyang'ane nokha. Ndipo pamene ife tikuyang'ana mu galasi lalikulu la Mulungu la Mawu Ake, tiyeni wathu. . .tithe kudzizindikira tokha ndi ena amene titawakambe, ena mwa anthu a nthawi zina. Ndipo ine ndikufuna kudziwona ndekha mu—mu galasi loyang'anira la Mulungu. Chifukwa, ngati chirichonse chingakuwonetseni inu pamene inu mwayima, ndi Bukhu *ili*. Palibe bukhu ngati Ili, chifukwa Ilo ndi lonse Choonadi. Ine sindikunena kuti mabukhu enawo si owona, koma ine—ine ndikudziwa kuti Ili ndi lowona. Ilo lonse ndi Choonadi, chifukwa Ilo ndi Mawu a Mulungu.

⁴⁰ Tsopano, Yesu anatipatsa ife Chitsanzo cha chimene ife tikuyenera kumayang'anapo, pamene Iye ananyezimiritsa Moyo Wake kwa ife kupyolera mu Mawu, chimene ife tikuyenera kuchiwona. Pamene ife tiyang'ana mu galasi la Mulungu,

tikuyenera kumadziwona tokha tikuzindikiritsidwa ndi Iye. Chimenecho ndi Chitsanzo changwiro.

⁴¹ Tsopano, koma ife tikupeza kuti, pamene ife tikudutsa kudutsa mmoyo, kuti khalidwe lathu limawumba chithunzi chimene ife tiri. Aliyense amadziwa zimenezo. Inu, momwe inu mumakhalira, momwemonso ndi khalidwe lanu, limakuwumbani inu ku chimene inu muli. Tsopano, mwawawonapo anthu amene inu mumangokonda kukhala pafupi nawo, komabe mwinamwake iwo sangakhale kwenikweni mu—mu gulu lanu la anthu. Ndipo, komanso, iwo akhoza kukhala a mtundu wosiyana, achikuda, kapena abulauni, kapena achikasu. Koma pamangokhala chinachake chokhudza khalidwe limenelo, kuti umangokonda kukhala mu kukhalapo kwawo. Chifukwa munthu aliyense ndi a—mphamvu yaying’ono ya iyemwini, ndipo inu—inu mumatulutsa kachikhalidwe pozungulira.

⁴² Ndiyeno munawawonapo anthu amene anali anthu olemekезeka, komabe inu munali okondwa nthawizonse kuchoka kwa iwo. Izo ndi basi iwo—iwo amalenga chikhalidwe choterocho pozungulira pamene inu muli. Palibe chowatsutsa iwo, iwo ndi anthu abwino, koma inu basi simumakonda chikhalidwe chimenecho, iwo, iwo ali. . . iwo alimo. Ndipo chikhalidwe chawo chimalenga chirichonse chimene iwo ali, chimawapanga iwo chimene iwo ali.

⁴³ Pamene Mulungu anayang’ana pa chirengedwe Chake chotayika, Iye atatha kuchipanga icho ndi kuchikonza icho basi momwe Iye ankafunira icho. . . Ndipo ine—ine ndimakonda kuyang’ana pa icho mu chiyambi chake. Ine—ine ndimakonda kupita kunja, chifukwa, kumeneko, izo ziyenera kuti ndi momwe Iye amafunira izo, kapena Iye sakanazipanga izo mwanjira imeneyo. Ndipo ife timabwera pamene ndi kudzapotoza izo, ndi kupanga chinachake kuchokera mwa icho chimene sichimamukondweretsa Iye. Koma, khalidwe Lake lokonda, linawumbidwa; Mulungu, powona kuti Lake—kuti dongosolo Lake lalikulu ndi kulengedwa kwa mtundu wa anthu kuti akhale pa dziko lapansi, ndi kuti azikhala mwa mtendere, ndi kuti asadzafonse, osadzadwala konse kapena kukhala ndi kupweteka kwa mtima kapena kudandaula kulikonse. Oh, ndi—ndi njira yotani imene Atate anayipereka kwa ife! Ndipo chimenecho chinali Chake—icho chinali chokhumba Chake kuti, kuti ife tizikhala mwanjira imeneyo. Iye sanafune kuti ife tizikhala mmawonekedwe akufa monga momwe ife tiririmu. Ichi, ndi a—a chikhalidwe chimene dziko lirimo lero, si chikhumbo konse cha Mulungu. Iye sankatanthauza zimenezo, nkomwe.

⁴⁴ Koma pamene Iye anawona kuti chirengedwe Chake chinali—chinali chitagwa, tsopano khalidwe Lake lomwe lokonda linadziwumba llolokha mwa Munthu wa Khristu.

Khalidwe kumene la Mulungu la chikondi anadziwonetsera Iyemwini mwa Munthu, Khristu. Monga Paulo akuyankhula apa, “Kusaganiza kukhala cholanda, koma anadzipanga Yekha wofanana, wofanana ndi Mulungu, kani.” Mukuona? Khalidwe Lake Lomwe linawumba Munthu wa mtundu umenewo. Oh, palibe amene akanakhoza kuchita izo koma Mulungu. Izi zinachitika kuti Iye alipire chilango cha kugwa kwa chirengedwe Chake. Mukuona? Iye . . .

⁴⁵ Pankayenera kukhala chinachake choti chipulumutse chirengedwe ichi. Ndipo palibe chimene chikanapulumsa icho, chifukwa mtundu wapamwamba kwambiri wa chirengedwe Chake unali utagwa, ndipo chirichonse cha pansi pa icho chinagwa limodzi ndi icho, chifukwa icho chinagwa. Panali chinthu chimodzi chokha chinatsalira, chimene sichinagwe, ndipo icho chinali Mulungu, miyamba. Kotero chinachake cha mmiyamba chinkayenera kuti chitsike kuti chidzawombole cholengedwa ichi, chifukwa panalibe chirichonse kuno chimene chikanalenga icho. Ndipo chikondi cha Mulungu mwini kwa dziko lapansi chinalenga khalidwe lowonetseredwa mwa Khristu. Iye anali khalidwe la Mulungu. Iye anali chifaniziro chowonetseredwa cha Mulungu. Mwa Iye munali Mulungu, Mulungu mwa Khristu, akudziwulula Yekha ku dziko lapansi. Ndipo palibe chikondi chimene chikanakhala chachikulu kuposa chikondi chimenecho, kuti, Munthu woteroyo akanadzakhala chimene Iye anachita, kuti adza—kutidzawombole chimene chinatayika.

⁴⁶ Izo zikuyenera kutero, lingaliro lokhalo apo pomwe, likuyenera kuyika Phoenix ndi dziko lonse ku manyazi, kuti tiwone chikhalidwe chimene ife tagweramo. Ndipo chimene . . . Mulungu, akudziwonetsera Yekha, kuti apange dongosolo la chiwombolo, kuti—kutidzawombole khalidwe lathu lakugwa ili.

⁴⁷ Izi zinachitika kuti chilangocho chiripiridwe, chifukwa—chilangocho chinali imfa. Ndipo wina amene anali pansi pa chilango cha imfa sakanatha kulipira chilango cha mzake amene analinso pansi pa chilango cha imfa. Kotero pankayenera kuti pakhale Winawake wobwera yemwe anali mfulu ku imfa, kuti adzalipire chilangocho. Ndipo panalibe wina akanabwera koma Mulungu, chifukwa Iye anali Mmodzi yekhayo amene anali mfulu ku chilango cha imfa.

⁴⁸ Tsopano, chotero, khalidwe Lake lokonda la chikondi, oh, kwa ife, zimenezo—zimenezo zikumveketsa bwino Yohane 3:16. “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapereka Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense amene akhulupirira mwa Iye asatayike, koma akhale nawo Moyo Wamuyaya.” Mulungu, akudziwonetsera Yekha, ndi kusandulika Munthu, kuti Iye adzakhoze kukhala nawo pa Iye mawonekedwe a chirengedwe Chake. Mwa kuyankhula kwina, Iye anasinthia chihema Chake. Iye anachitambasulira icho pakati pa anthu.

49 Ndipo khandalo, Yehova, kulira modyera ng'ombe, kodi mungalingalire zimenezo? Izo zimayenera kudzidzimutsa mitima ya okhulupirira. Ndipo izo zonse zinachitidwa... Kodi inu mungalingalire, Yehova kukhala khanda mo—modyera ng'ombe, mu pa—pa mulu wa manyowa? Kodi inu mungalingalire zimenezo? Kodi inu mungalingalire, Yehova wamng'ono akusewera ngati a—ngati mnyamata? Ichu ndi chitsanzo. Kodi mungalingalire, Iye ngati wa mmadini? Kodi inu mungalingalire, Iye ali mwa kalipentara? Ndipo kodi inu mungalingalire, Iye ali mu kumvera kotheratu kotero kwa Mulungu, akufa pa mtanda, kuti adzawombole chirengedwe Chake chakugwa? Umenewo ndi mtundu wa chikondi chimene Mulungu anali nacho. Ndipo Iye ankayenera kukhala chimenecho, ndi cholinga chakuti afe, kuti adzagwire mbola ya imfa.

50 Tsopano, ine ndikukhulupirira, mausiku angapo apitawo ife tinali kufotokoza chinachake mwa dongosolo limenelo, pamene Iye anabwera. Ndipo Iye anatumiza aneneri ndi anthu opambana, ndipo Iye anatumiza Mose ndi aneneri, ndipo Iye anapereka malamulo. Koma onsewa sakanatha kuwombola, chifukwa iwo anali akanali anthu pansu pa chilango cha imfa. Ndipo iwo sakanatha kulipira chilango cha imfa, ngakhale kuti iwo anali mizati-yolozera kwa Mmodzi wangwiroyo akubwera, chifukwa iwo sanali angwiroyo. Koma pamene Uyu anabadwa, Iye anabadwa wopanda tchimo.

51 Mulungu, Yehova, anamuphimba namwali ndipo analenga Khungu la Magazi, ndipo pamene iye anabadwa, iye anali Mwana wa Mulungu. Mwa kuyankhula kwina, iye anali kachisi. Iwo anali malo okhalamo amene Yehova akanakhoza kumakhala pakati pa anthu Ake ndi kudzifotokoza Yekha, chimene Iye anali.

52 Ndi chitsanzo chotani, momwe kuti Mulungu woyera anawonetseredwa, ndipo kenako anadzatenga malo a wantchito, kudzatsuka mapazi! Ndipo anayankhula, kuti, “Mbalame ziri ndi zisa, ndipo—ndipo ankhandwe ali ndi mphanga, koma Ine ndiribe poyakapo mutu Wanga.” Ndiye, ndi chitsanzo chotani! Kodi moyo wathu unganyezimiritse motani, kwa Wake? Ndipo Iye anapanga chitsanzo cha chimene ife tikuyenera kuchita, momwe ife tikuyenera kumakhallira. Iye tiyenera tizimuwona Iye pamene tiyang'ana pa galasi. Kumuwona Khristu, galasi la Mawu Ake, momwe Iye anachitira izo chifukwa cha chikondi.

53 Ndipo ife tinapereka sewero laling'ono usiku wina, la Khristu akupita ku Gologota, ndi momwe kuti mphondero, za Magazi Ake akuyenderera kumbuyo Kwake, kumene Iye anali atakwapulidwa, ndi kuzunzidwa, ndi kutunduzidwa. Ndipo zonsezi, chifukwa cha inu. Iye analibe tchimo. Iye analibe tchimo, koma iye anapangidwa tchimo pokhala nsembe ya tchimo.

⁵⁴ Ndipo tsopano Mulungu ankayenera ku—kudziwulula Yekha mu zikhumbo Zake, mwa Munthu uyu wotchedwa Khristu, kuti atengere imfa pa Iyemwini. Monga Yehova, Iye sakanafa, kotero Iye ankayenera kuti adzilengere Yekha thupi. Ndipo palibe mkazi amene akanakhoza kubala thupi limenelo. Kotero khalidwe Lake Lomwe. . . Amen. Ndikhululukireni ine. Pamene ine ndiganiza za zimenezo! Khalidwe Lake linawonetsera Umunthu wokondeka uja wa Yesu Khristu. Palibe mkazi amene akanakhoza kulibweretsa ilo. Amayi ake a Mose, iwo, Yokebedi, iwo anali mkazi wopambana, ndipo momwemonso Rebekah ndi ena ambiri a akaziwo, koma palibe mmodzi wa iwo akanakhoza kutulutsa mtundu uwu wa khalidwe, chifukwa ilo linabwera kudzera mu kugonana pogwiritsa ntchito anthu okugwa. Koma Mulungu anawonetsera thupi Lake Lomwe, malo Ake okhalamo. Ndi chifukwa chake Iye anali Mwana wa Mulungu, chifukwa palibe china chirichonse chimene chikanakhoza kuwonetsera ilo. Koma khalidwe Lake lomwe Lauzimu linawonetsera kachisi uyu, kuti adzadzifotokozere Yekha mmenemo.

⁵⁵ Ndipo, komabe, Iye anadzichotsa Yekha ku chinthu chachikulu chimene Iye anali. Ndipo pa kubadwa Kwake, Iye akanakhoza kubwera ndi sawasha yathunthu ya Angelo. Iye akanakhoza kubwera ndi magaleta ndi Angelo a Kumwamba, koma Iye anabwera mwa njira ya khola. Icho ndi Chake—chikondi Chake, kudzitsitsa Yekha mpaka kwa wotsikitsitsa.

⁵⁶ Tsopano, inu muphunzire khalidwe limenelo pang’ono pokha ndipo kenako mudziyang’ane nokha, ndipo ine ndidziyang’ane ndekha. Koma, icho ndi chimene Iye anali, ndi Yemwe Iye anali, ndipo icho ndi chifukwa chimene Iye anali, kuti adzakupulumutseni inu. Iye anatenga. . . Iye anadzakhala inu, kuti inu mudzakhoze kukhala Iye. Iye anatenga katundu wanu wa tchimo.

⁵⁷ Chotero, pamene ife tibwera kudzakumana naye Iye, siti yenera kuti tiyime. . . Ife sitingakhoze kuyima mu Kukhalapo kwa Mulungu. Palibe njira yoti ife tingachitire zimenezo. Koma pamene ife tiyima mwa Iye, mwaona, Iye amakhala kuti waizindikira kale Nsembeyo. “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa mwa Iye Ine ndimakondweramo.” Iye anzindikira zimenezo. Panalibe chilema pa Iye. Ndipo, komabe, Iye anavutika ndi mayesero monga munthu wina aliyense. Komabe, Iye ananyozedwa. Iye anasekedwa. Iye anazunzidwa, kuyambira ora limene Iye anabadwa mpaka ora limene Iye anadzafa, ndipo komabe Iye anabwezera zabwino kwa zoipa.

⁵⁸ Inu simungathe, palibepo njira, yotulutsira Khalidwe longa limenelo; kokha, povomereza Khalidwe limenelo mwa inu. Mpingo sungathe kuchita zimenezo. Kachikhulupiriro sikangachite zimenezo. Chipembedzo sichingachite zimenezo. Maphunziro sangachite zimenezo. Kuyenera kukhala Kubadwa. Iko kuyenera kukhala a—kufa, ndi kumulola Mulungu kuti

alowe, mwa chisomo cha Khristu, kuti awumbe mtundu uwu wa khalidwe mwa inu, kuti inu mudzakhale Iye, ndipo moyo wanu ndi Wake udzakhale wofanana, zikatero inu ndi ana aamuna ndi aakazi a Mulungu.

⁵⁹ Ndiye, pamene Iye ankapita pamwamba pa phiri, ndipo mtanda Wake unali ukukwakwazika mu mphondero, oh, ndikanakonda ndikanakhala wojambula, ndikanakonda ndikanakhala, ndikanakhoza moganiza kukujambulirani inu chithunzi chaku Gologotha, cha ora lowopsya kwambiri limenelo limene dziko linayamba lalidziwapo, ndipo komabe, iwo sankazindikira chimene chinkachitika, mamillioni sankazindikira.

⁶⁰ Ndipo kodi ndingatembuzire chithunzicho ku chimene ndinanena sabata ino? Ife tikulowanso kachiwiri mu ora lowopsya, nthawi yowopsya. Ndipo Phoenix ndi dziko lapansi zikusambira, ndipo mipingo ikudzisambitsa yokha, mu chidziko, ndi mu ziwonetsero za ku Hollywood, wina kumuposa mzake. Ndipo mamembala athu akukhala achidziko. Zikuwoneka kuti iwo sakuchigwira chithunzicho, komanso kuyipa kwake, ndi vumbulutso, la kuwonekera kwa Mwana wa Mulungu mmasiku otsiriza ano.

⁶¹ Iyo inali nthawi yowopsya bwanji! Iwo ankangodziwa kuti kunali chigawenga, pansu pa chilango cha boma, anali woti akafa mmawa umenewo. Ndizo zonse zomwe zinali kwa iwo.

⁶² Ndizo zonse zimene Izo ziripo lero, kwa anthu, pamene iwo amva Uthenga. “Munthu wina wakuthengo; woyera wodzigudubuza wina; kapena chidempete china chachipembedzo.” Ndipo sindikunena kuti kulibeko zidempete za chipembedzo. Koma kodi inu mumangodziwa kuti... Iwo amawatcha iwo, “Osamvetsetseka.” Chabwino, mvetserani. Aliyense amene akukhala molondola ndi wosamvetsetseka, kwa dziko lamakono ili. Ndife tonse osamvetsetseka, monga ife tinganenere. Ndipo mukhululukire kafotokozedwe kachidziko kameneko, koma iyo ndi njira yokhayo imene ndimaidziwa kuti inu mukanadziwira chomwe ine ndikuchikamba; mwaona, basi wosamvetsetseka, wachirendo, munthuyo.

Yesu anali Munthu wa mtundu umenewo.

⁶³ Aneneri anali anthu a mtundu umenewo, amene ankabwera mu m’badwowo pamene chirichonse chinali chikufika kumathero omasuka. Ndipo aneneri ankabwera ndipo ankadzagwira malo omasuka amenewo, ndipo ankawabwezeretsa iwo ndi kuwakankhira iwo pa nkhope za anthu, ndipo ankawauza iwo, “Mulungu yemweyo amene inu mumadzinenera kuti mukumutumikira adzakuwonongani inu, chifukwa inu mwachoka ku dongosolo Lake. Imeneyo ndi njira yokhayo imene Iye angakupulumutsireni inu.” Ndipo iwo nthawi zonse amakhala osamvetsetseka.

⁶⁴ Ndipo, lero, pamene ife timva Uthenga wa Mulungu ukubwera, ife timaganiza kuti Iwo ndi kuluku winawake, kuphokosera, kapena chinachake. Ndipo kumeneko, kuli zambiri za izo mdziko: zochitika, kupanga ndalama, osakhudzidwa, anthu omwe ali ndi zomverera ndi—ndi kumayankhula ngati kuti anali Ambuye. Ambuye nthawizonse mowona amadzizindikiritsa Yekha. Mukuona? Ndipo zindikirani.

⁶⁵ Koma, mmenemo, kodi inu mumadziwa kuti zinthu zonsezo zimayenera kubwera? Ndithudi. A—duwa limayenera kukhala ndi minga zake. Njere mu a—mu mtedza imayenera kuphimbidwa ndi zobaya. Inu mumayenera kukumba zobayazo kuti mukafike pansu ku njere. Ife timangolephera kuziwona zinthu zimenezo. Ngale, a—a—zitsulo ndi ngale, ndi ndalama, siliva ndi golide m’mapiri awa, zinakutidwa ndi dothi, kudzazidwa ndi golide wopusitsa ndi miyala ina imene imayendera limodzi ndi izo. Ife timayembekezera zimenezo. Iwe umayenera kukumba zimenezo. Pamene wofufuza apeza chimene amachitcha “golide wafumbi,” ndi fumbi, koma ndi . . . Iwo amawona izo. Izo zimaimirira, mmenemo, apo pamakhala mthunzi wa mpita wawukulu penapake.

⁶⁶ Ndipo pamene ife tiwona anthu awa lero odzinenera kuti ndi Akhristu, ndi kumangokhala mwanjira iliyonse, icho ndi chiyani? Ndi golide wopusitsa. Pali phata lalikulu penapake. Pamene ife timuwona winawake akuchita ngati ali ndi Mzimu Woyera, pamene iwo alibe, ndipo nkumakhala moyo wosiyana, ndi umboni chabe kuti pali phata lenileni la Mzimu Woyera umene ukhoza kutsanuliridwa, umene ukhoza kupereka zinthu zimene Iye analonjeza. Ife tikuyenera kukhala okhudzidwa kwambiri ndi olemkeza.

⁶⁷ Yesu, pa ulendo Wake wokwera. Mdierekezi nthawizonse ankakaikira Izo kukhala woposa mneneri. Iye sankakhulupirira kuti Iye anali Emanuele. Mulungu akuwonetseredwa mwa Mwana Wake Yemwe, Iye ndi Mwana Wake kukhala Mmodzi, bwanji, iye sankakhoza kuziwona zimenezo. Mulungu akanakhoza bwanji, Mlengi wamkulu, akanakhoza bwanji kuyima ndi kumulola winawake kuti amuwuze Iye, “Chabwino, ngati iwe uli Mwana wa Mulungu, lamulira miyala iyi kuti isanduke mkate”?

⁶⁸ Ndipo Iye akanakhoza bwanji, mu bwalo la Pilato, pamene a . . . Mundikhulukire kanenedwe kakeko; koma pamene zinthu zinafika povuta, monga tingazitchulire izo. Ndipo apo Iye anali ali ndi chinsanza mozungulira nkhope Yake, ndipo—ndipo asilikali Achiroma akulavulira pa nkhope yake, ndi kumwetula ndevu, ndipo Magazi akukhuthuka. Ndipo ali ndi chisoti chaminga pamutu pake. Ndipo atamenyedwa kale, ndipo Magazi Ake akuyenderera mwaufulu ku mbali Zake. Ndipo Satana akupenyererera zimenezo. Ndipo kenako anayika

chinsanza pankhope pake, ndipo asirikaliwo anamumenya Iye pamutu ndi ndodo, ndipo analandizana wina ndi mzake, anati, “Tsopano, ngati iwe ungewone masomphenya awa, ngati iwe uli mneneri, tsopano, iwe—iwe utiuze ife amene wakumenya iwe.” Ndipo Iye sanatsegule konse kamwa Yake. Kotero iwo anaganiza kuti. . .

⁶⁹ Satana anati, “Ameneyo, ameneyo sangakhale Mwana wa Mulungu. Izo sizingatheke basi. Iye sakanalolela zimenezo.” Koma ana a Mulungu amalolela chirichonse bola ngati iwo akudziwa kuti akuchita chifuniro cha Mulungu. Ndipo icho ndi chimene Iye anabwera kudzachita. Kutsutsidwa!

⁷⁰ Tsopano, ndi Uthenga wathu, kodi ife tingayime pa galasi loyang’anira la Mawu a Mulungu ndi kumuwona Khristu akunyezimira mmiyoyo yathu yomwe? Kodi tingapirire zoterozo, ndi chitonzo cha Uthenga umene ife tikuwumira pano? Winawake akhoza kunena chinachake za Iwo, ndipo komabe inu osatsegula pakamwa panu basi ndi kunena kanthu za izo. Iye anali chitsanzo, chifukwa Mulungu anali akunyezimiritsa khalidwe Lake mwa Iye. Ndiyeno ngati ife tiri ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, Mulungu amanyezimiritsa khalidwe Lake mwa ife, zikatero ife timakhala ngati Iye. Icho ndi chokhumba cha mtima wanga. Ine ndikuganiza icho ndi chokhumba cha wokhulupirira aliyense, ndi kukhala mochuluka monga Iye.

⁷¹ Ndiyeno panjira yopita ku phiri, pamene Satana anati, “Chabwino, imfa, tsopano iwe ukudziwa kuti ndiri nawe mu ulamuliro wanga. Ndipo pamenepo Iye ali. Ife potsiriza tinamutopetsa Iye. Izo zinafika pa malo amene Iye—Iye anafika kumapeto a nzeru Zake. Iye sakudziwa choti achite kenanso. Iye anadzakhala chitonzo pakati pa anthu. Uthenga Wake unagwera mu mphepo. Ndipo tsopano boma lamugwira Iye, ndipo Iye wagonjetsedwa. Iye si Mulungu. Pita kumusi uko ndipo ukazike mbolayo mwa Iye. Ukamuchotsere Iye moyo.”

⁷² Ndipo panjira yokwera phiri, pamene njuchiyo inayamba kulira momuzungulira Iye. Koma icho ndi chifukwa chimene Iye ankayenera kukhala woposa munthu. Ngati Iye akanakhala munthu, kapena mneneri chabe, kapena chirichonse chocheperapo pa Mulungu, ngati Iye akanakhala chimenecho, imfa ikanamulumu Iye ndipo Iye akanagona mmanda.

⁷³ Koma njuchi ya imfa ili ngati kachiroombo kalikonse kamene kali ndi mbola. Ngati mbola yake ilowa mkati, masiku ake oluma amatha. Iyo imakokera mbola yake kunja.

⁷⁴ Chabwino, zikanakhala kuti mnofu wa munthu unali mu—mawonekedwe a tchimo, wobadwa mogonana pansu pa themberero, ndiye imfa ikanaluma mnofu umenewo, mbolayo ikanatha kubweranso ndi kudzalumanso wina.

⁷⁵ Koma pamene iyo inaluma mnofu *umenewo*, iyo inatulutsira mbola yake panja. Iyo ilibenso mbola. Iye anali Mulungu mu

thupi, akukhala pakati pa anthu. Masiku ake oluma anatha. Ndi chifukwa chake Mulungu ankayenera kudziyemiziritsa Yekha mu thupi, lomwe liri, ife timalidziwa ngati Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu. Ndipo Iye anachita zimenezo ndi cholinga chakuti Iye adzakhoze kuchotsa chilangocho.

⁷⁶ Chifukwa, inu mukuwona tsopano, ife tikupita ku gawo lina la Lemba. Koma inu mukuwona tsopano chifukwa chimene Munthu ameneyo anali woposa mphunzitsi chabe, monga anthu amanenera kuti Iye ali lero, namatetule, kapena Munthu wabwino, kapena mneneri. Iye anali Emanuele. Iye anali Mwana wa Mulungu, amene ali Yehova Mulungu atawonetseredwa mu zikhumbo Zake za kudziwonetsera Iyemwini mu thupi lomwe Iye analimanga, Iyemwini. Amen. Izo zinanyedzimiritsa. Ndipo chikhalidwe cha tchimo cha munthu sichikanakhoza kuchita chinthu chimene Iye anachita. Mukuona? Koterokoyenera kukhala Mulungu akupanga Ake. . . akudziyemiziritsa Yekha mwa Munthu, akupanga kalilole, kuti ife tikhoze kudzamuwona Munthu wangwirowa, amene ali Khristu. Inde.

⁷⁷ Ichi, pochita chimenecho, ananyedzimiritsa khalidwe Lake lolemekezeka, la chikondi. Mwaona, mwa Iye munali chikhumbo chokhala Mpulumutsi, ndipo icho chinkayenera kudziwonetsera chokha. Ndipo Iye sakanakhala Mpulumutsi ndi kukhala munthu wobadwa mwachibadwa. Iye ankayenera kukhala woposa munthu. Ndipo Iye anali. Iye anali Mmodzi yekhayo amene akanatha kuchita ichi, mochulukira kuti Iye anali wopanda tchimo mwachibadwa.

⁷⁸ Iye anali Mulungu mu Mawu. Tsopano, Yohane Woyera, mutu wa 1, akufotokoza zimenezo. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi.” Mulungu anadzandulika thupi pamene Iye anayimiridwa, kapena pamene Iye anadziwonetsera Yekha ku dziko lapansi, mmawonekedwe a Mwana Wake, Munthu wa Yesu, Mwana wa Mulungu. Mulungu anadziwonetsera Yekha mwa Munthu ameneyo.

⁷⁹ Kodi Yesu sananene kuti, “Atate Anga ndi Ine ndi Mmodzi. Atate Anga amakhala mwa Ine. Si Ine amene ndikuchita ntchitozi. Ndi Atate Anga. Iye amakhala mwa Ine. Ine ndiribe ulamuliro wa Ine ndekha. Iye amachita zimenezo.” Kasupe wa Mulungu wa Mawu, akuwonetseredwa! Amen. Ine ndikumverera mwachipentekoste. Inde.

⁸⁰ Iye anali wopanda tchimo mwa chibadwa, ndipo icho ndi chinthu chokhacho chimene chikanakhoza kuwonetsera Mulungu wopanda tchimo ameneyo, Mawu, Mawu kukhala Mulungu. Ndipo mawu ndi ganizo lofotokozedwa. Ndipo pamene Mulungu anaganiza za kholo, Iye anafotokoza lingaliro Lake, ndipo—ndipo Khristu anali chiwonetsero cha Mulungu. Amen. Inu mukuziwona zimenezo? Iye anali chiwonetsero cha Mulungu,

kuti Mulungu adzakhoze kukhala ife ndi kudzakhala monga ife timakhalira, komabe akuwonetsera mwanawiro chimene munthu wawiro akuyenera kukhala, mwanawiro. Iye anali Mawu a Mulungu akuwonetseredwa ndi kutsimikiziridwa moyenera, kuzindikiritsidwa. Pamene Iye anayima pano pa dziko lapansi, Iye anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine.”

Ndipo Iye anati, “Ndani mwa inu amene anganditsutse Ine za tchimo?”

⁸¹ Ine ndikufuna kuti nditsegule chimenecho pang’ono pokha kwa inu, ngati ziri zololedwa. Inu mwaona, *tchimo* ndi “kusakhulupirira.” Ziripo zinthu ziwiri zokha, mipita, zomwe mungakhalire nazo moyo. Chimodzi cha izo ndi chikhulupiriro, ndipo chinacho ndi kusakhulupirira. “Iye amene sakhulupirira watsutsidwa kale.” Kusuta, kumwa mowa, kuchita chigololo, kunama, kuba, kunyengezera kwachithupithupi, zinthu zimenezo ndi zikhumbo za kusakhulupirira. Ngati inu mukanakhala wokhulupirira, inu sibwenzi mukuchita zinthu zimenezo. Ayi. Iwe umachita zimenezo chifukwa ndiwe wosakhulupirira.

Oh, inu—inu mukuti, inu mukuti, “Oh, koma ndine wokhulupirira.”

⁸² “Koma ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Mukuona? Zanu—zochita zanu zimayankhula mofuula kuposa zomwe kuvomereza kwanu kumatsimikizira. Mukuona? Pamene inu simukhulupirira Mawu a Mulungu, ndi kuwawerengera Iwo ngati chinachake chimene chinapita, kapena kutenga bukhu lina mmalo mwa Iwo, ndi kumati, “*Ichi* ndi chabwino basi monga Icho,” izo zimasonyeza kuti ndinu wosakhulupirira. Uko nkulondola. Inu ndi—inu simuli. Ndipo ngati mukanakhala, ndiye inu mukanakhulupirira Mawu a Mulungu. Iwo akanatero...Iye akanadziwonetsera Iyeyekha kupyolera mu Mawu Ake.

⁸³ Tsopano, Iye anali Mawu a Mulungu owonetseredwa. Ndipo Iye anati, “Tsopano, ngati inu simugandikhulupirire Ine,” anati, “mukhulupirire ntchito zimene Ine ndikuzichita. Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo ndicho chinthu chomwecho chimene chikunena Amene Ine ndiri.” Oh! Ndikudabwa ngati...?... “Mwaona, Ameneyo ndi Amene akunena Yemwe Ine ndiri. Malemba akunena Amene Ine ndiri.”

⁸⁴ Ndipo ndiroleni ine ndizitengere izo patsogolo pang’ono, inu mutero? Malemba ndi amene amanena chimene inu muli. Iwo amakufotokozani inu ndi kundifotokoza ine. Malemba amanena chimene ife tiri. Izo zimafula kwambiri moti mawu athu sangamveke nkomwe. Moyo wathu umayankhula mokweza

kuposa mawu athu, mwaona, ndipo ndiyo njira ya Mulungu yotilolera ife kuwona chimene ife tiri.

⁸⁵ Yesu ananena chinthu chomwecho. “Iwo ndi Amene akuchitira umboni za Ine. Iwo akutsimikizira chimene Ine ndiri. Ndipo ndani wa inu amene anganditsutse Ine za kusakhulupirira, tchimo? Ngati sindinachite moyenera...” Mvetserani, ine ndikuyankhula za kudziyang’ana nokha. “Ngati Ine sindinadzizindikiritse Ndekha moyenera monga kukhala chimene Mawu ananena kuti ine ndikanadzakhala!”

⁸⁶ Ndikudabwa ngati ife Akhristu tingaganize zimenezo usikuuno. Ndikudabwa ngati ife tingayang’ane pa galasi loyang’anira la Mulungu, za zomwe zimafunikira kwa Mkhristu, ndi kudzizindikiritisa tokha mwanjira imeneyo. Ndikudabwa ngati ife tingatero. Ine ndikudabwa ngati ife tingathe kudzizindikiritisa tokha usikuuno ndi Yohane 3:16, ndi, oh, mitundu ina yonse ya Malemba; Marko mutu wa 16, ndi malo ena onsewa, izo, ndi mpaka mu—mu Agalatiya, ine ndikukhulupirira, ndi—ndi malo osiyanasiyana, Atesalonika Wachiwiri, pamene zipatso za Mzimu, ndi zina zotero. Ndikudabwa ngati tingadzizindikiritse tokha.

⁸⁷ Yesu anati, “Ndani wa inu amene angathe kunditsutsa Ine, kuti ine sindinachite ndi kupanga ndendende basi zomwe Malemba ananena kuti ine ndikanadzazichita.” Palibe amene anakhoza kunena liwu, chifukwa Iye anali moonadi atadzizindikiritisa Yekha.

⁸⁸ Ndipo iwo, monga iwo amachitira nthawizonse, wodzipangitsa-kukhulupirira anali atamudzindikiritisa Iye ngati Bezebule, mzimu woyipa. Pamene Iye anadziziwitsa Yekha mu kuzindikira kwa mzimu, kuti Iye anali Mesiya, kenako iwo anati, “Umenewo ndi mzimu woyipa mwa Iye, ukuchita zinthu izi.” Kotero, inu mwaona, Iye anatsimikiziridwa bwinobwino. Pamenepo sipakanakhala kulakwitsa.

⁸⁹ Mkazi wamng’ono pa chitsime sana—sanapange kulakwitsa kulikonse. Iye anati, “Bwana, ife tikudziwa, kuti pamene Mesiya adzabwera, Iye adzachita zinthu zimenezi, koma Inu ndi Ndani?” Iye. . .

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

⁹⁰ Ndipo Munthu amene angakhoze kuchita chinthu chonga icho ndithudi anganene Choonadi. Choonadi cha Mulungu chinali ndi Iye. Ndipo iwo anatumidwa, ngati mneneri adzawuka ndipo—ndipo nkuchita, nkudzanena chinachake, ndipo chimene wanenacho nkudzachitika, iye ankazindikiritidwa ngati mneneri. Ndipo iye anali atamuzindikira Iye ngati mneneri, ndipo anamufunsa Yemwe Iye anali. Ndipo Iye anamuwuza iye, ndiye izo zinakhazikitsa izo. Iye anathamangira mu mzinda ndipo anati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wandiuza ine zinthu.” Panalibe kulakwitsa za zimenezo.

Filipo analibe cholakwika.

⁹¹ Ngakhale, pamene, Nataniele, kani, pamene Filipino anayesera kumuwuza iye chimene chinachitika pamene Iye anakomana ndi Simoni, koma, pamene Nataniele anabwera, iye anali mu kukayikira pang'ono.

⁹² Koma pamene iye anamuwona Yesu, ndipo Yesu anati kwa iye, “Taonani m’Israeli, amene alibe chinyengo.”

Iye anati, “Rabbi, kodi Inu munandidziwa ine liti?”

⁹³ Iye anati, “Filipo asanakuyitane iwe, Ine ndinakuwona iwe.” Panalibe—panalibe njira yotheka yochitira cholakwika.

⁹⁴ Iye anati, “Rabbi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli.”

⁹⁵ Yesu anati, “Chifukwa ine ndakuwuzwa iwe zimenezo, iwe wakhulupirira. Iwe ukhoza kuwona zazikulu kuposa zimenezo tsopano.”

⁹⁶ Khalidwe lake lopanda tchimo linawonetsera Mawu a Mulungu. Mukuona? Iye anali Mawu, kotero Mulungu anadziwonetsera Yekha mwa khalidwe lopanda tchimo limenelo.

⁹⁷ Ndiloleni ine ndiyime apa mphindi chabe. Ine sindikufuna kukusungani inu nthawi yaitali kwambiri, koma izo zikungowoneka zabwino kwambiri, kwa ine, kuyankhula kwa anthu.

⁹⁸ Zindikirani, onani, khalidwe Lake lopanda tchimo linawonetsera chimene Iye anali. Iye, ndiye, ngati khalidwe Lake lopanda tchimo, Mulungu anadziwonetsera Yekha kudzera mu khalidwe lopanda tchimo limenelo, izo zikuwonetsera kuti chikhalidwe chathu ndi choyipa. Ndipo ziribe kanthu momwe ife tingayetsere kulisokerera ilo, kapena mochuluka bwanji momwe tingayetsere kulipatsa ilo zitupa ndi zinthu zina, ilo liyenera kukhala lopanda tchimo monga Iye anali, ndipo kenako Mawu a Mulungu akhoza kumayenderera kupyolera mwa ilo.

⁹⁹ Izo sizikutanthawuza ungwiro mwa inueni. Inu simungathe kukhala chimenecho. Koma, inu mwaona, ngakhale anthu athu akuchoka ku machitidwe a chiyero. Ife tayamba kulekelera zogwirira zambiri. Mukuona? Ife tikuyenera kubwera ku malo amenewo a chodzinenera chathu. Iye ndi chitsanzo chathu, ndipo Iye ndi Wonyamula tchimo lathu. Ndiyeno ngati ife tidzinenera kuti Iye ndi Wopangamtendere wathu, Iye ndi Chitetezero chathu, ndiye ngati ife tidzinenera zimenezo, ndiye izo zikuyenera kumunyedzimiritsanso Iye kwa ife. Ndipo ife ndi kalata yolembedwa, kalilole woyang’anirapo, kuti anthu akhoza kumuwona Khristu mwa ife. Ndipo tsopano, ngati iwo sakutero, ndiye ndife—ndife—ife tikuyang’ana pa chinachakenso, ndipo ife sitikuyang’ana kwa Iye. “Yang’anani kwa Iye, malekezero onse a dziko lapansi, ndipo mukhale moyo.” Njira yokhayo imene inu mungakwanitsire.

¹⁰⁰ Uchimo wake...khalidwe lopanda tchimo linawonetsera Mawu a Mulungu, mochuluka kwambiri, mpaka kuti Iye ndi Mawu anali Mmodzi. Iye ananena chomwecho. “Ine ndi Atate Anga ndi Mmodzi. Nthawi zonse ndimachita icho chomwe chimakondweretsa. Ine ndi Atate Anga ndi Mmodzi basi.” Iye anali wangwiro kwambiri mu chifaniziro cha Mulungu mpaka Iye ndi Mulungu anali chinthu chomwecho chowonetseredwa. Iye anali thupi, Mwanayo, amene ankawonetsera Umulungu wa Mulungu. Kotero izo zinamupanga Iye kukhala umulungu mwa Munthu, ndi cholinga chakuti amuwombole munthu. Mukuona? Iye ndi Mawu anali Mmodzi. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi.” Chotero, Iye ndi Mawu anadzakhala Mmodzi, kuti Mawu adzakhoze kuwonetsera ndi kukhoza kuwonetsera ku dziko Chitsanzo chimenecho cha momwe munthu akuyenera kukhalira.

¹⁰¹ Ndipo munthu sangakhale chimenecho mwa iyeyekha. Palibe njira yophunzitsira izo kwa iye. Palibe njira yojoinira izo. Palibe njira yobatizira izo. Palibe njira yochitira kalikonse kwa izo, kungomupha iye.

¹⁰² Ndipo mulole iye abadwe kachiwiri, ndipo Khalidwe latsopano libweremo. Ndiyo njira yokhayo, kupha chikhaliidwe chimenecho cha inumwini, kuti inu mukhoze kukhala... Ndipo mukatero Mawu amadzakhala chinthu chamoyo, Iwo amangodziwonetsera Okha kupyolera mwa inu. Mukuona? Ndiye kuti mukuyang’ana mu galasi loyang’anira, pamene anthu akukuwonani inu ngati kalilole. Chifukwa, inu mukudziwa, Mulungu wapanga njira. Anthu samawerenga Baibulo, kotero Mulungu wakupangani inu kukhala Baibulo. Inu muli. Zimene inu mumachita, anthu akuyang’ana pa inu.

¹⁰³ Mulungu anatumiza makalilole Ake, Kwake—Kwake—kuwonetsera Kwake kowonetseredwa kwa Iyemwini mwa aneneri, chifukwa Mawu ankabwera kwa aneneri. Ndipo iwo ankamufotokozera Mulungu mmenemo, chonchobe, uneneri wawo umene Mulungu anawapatsa iwo.

¹⁰⁴ Ndipo tsopano Mulungu anadziwonetsera Yekha kudzera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu, pamene Iye akutitengera ife mkati monga ana okhazikitsidwa, ndi kuyika Mzimu Wake mwa ife, kumafuula, “Abba, Atate.” Mukuona? Kapena, mwa kuyankhula kwina, “Mulungu wanga, Mulungu wanga!” Mukuona? Kenako Mzimu Woyera mwa ife, Mzimu wa Khristu ukumuwonetsera Yesu Khristu, ndipo anthu nkumayang’ana pa inu. Mukuona?

¹⁰⁵ Ndipo pamene iwo awona zachinyengo ndi chirichonse, nzosadabwitsa, ife tataya Mphamvu zathu. Mcherewo wataya kukoma kwake.

106 Oh, palibe khalidwe lina limene likanakhoza kuchita izi. Ayi. Chifukwa, Iye anali khalidwe lowumbidwa langwiwo la Mulungu.

107 Pakuti, ilo linali khalidwe lakugwa limene chirengedwe chonse chinali nalo. Anthu onse anali ndi khalidwe lakugwa. Ngakhale chirichonse chimene chinali pansu pa munthu chinagwa. Chirichonse chiri ndi khalidwe lakufa.

108 Ndipo Iye anali ndi khalidwe lamoyo, kotero Iye analifotokoza ilo mwa Khristu, ndipo Iye analipira mtengowo. Ndipo kenako chifukwa cha kumvera Kwake, Iye anamuwukitsa Iye pa tsiku lachitatu. Mukuona?

109 Ndipo kenako Iye amapereka kwa ife, izo zimatipatsa ife—umboni, izo zimatipatsa ife chitsimikizo, kuti, bola ngati ife tiri mwa Iye, ife tawukitsidwa kale ndi Iye. Ife sitidzawuka ndi Khristu; tinawukitsidwa kale ndi Khristu. Uko nkulondola. Ife tiri mwa Khristu tsopano. Ndipo ngati Khristu anawukitsidwa kwa akufa, kodi ife sitinawukitsidwe kwa akufa pamodzi ndi Iye? Amen. “Tsopano ife tikukhala limodzi mmalo Ammwambamwamba mwa Iye.” Oh, mai! Izo zikuyenera kukupangitsani inu Apresbateria kufuula. Uh-huh. Eya. Ndithudi. Zifanizo zowonetseredwa za Mulungu, zowumbidwa monga mwa kachitidwe ka Khristu, mpaka kuti dziko likhoza kumamuwona Iye mwa inu. Limenelo nde galasi loyang’anira loti muziziyang’anirapo.

110 Palibe chikhaliidwe china chikanatha kuchita zimenezo; icho chinali chakugwa. Ndipo Mulungu anazindikiritsa, penyani, Mulungu anadzizindikiritsa Yekha ngati Munthu, ndipo anadzitengera pa Iye mawonekedwe a tchimo. Tsopano, chabwino, osati tchimo, koma mawonekedwe a tchimo, kuti Iye athe kutenga tchimo la wochimwa, mwaona, ndi kulipira chilango cha ilo, ndi kumubwezera wochimwayo Moyo umene iye anali nawo iye asanagwe. Oh, mai! Ndi chikondi chotani chimene Mulungu wachiwonetsera kwa ife! Mukuona? Taganizani za zimenezo.

111 Ndipo tsopano kumbukirani, Yesu atatha kuchita izi, pamene panalibe wina aliyense amene akanakhoza kuchita izo, ife tikuyitanidwa. Tsopano, mpingo, taganizirani za izi miniti yokha. Ife tikuyitanidwa kuti tiwumbe khalidwe lathu kwa Lake, mwa chisomo Chake. Ife tikuyitanidwa, taganizani za zimenezo, kuti tikhale akhalidwe longa Lake. Ngati ife tiri okonzeka kuti tiyike khalidwe lathu pansu, ndi kuwumbidwa kumene ife tinali nako, “Ammutu, odzikuza, okonda zosangalatsa koposa okonda Mulungu, onenera zonama, ndi osadziletsa, onyoza iwo amene akuyesera kuchita molondola, okhala nawo mawonekedwe aumulungu ndi kumakana mphamvu ya Mawu.” Mulungu angakhoze bwanji kubwera mmalo ngati amenewo, pamene iwo akukana Mawu? Pamene,

Iye amayang'anira Mawu Ake, kuti awatsimikizire Iwo, kuti awapange Iwo kukwaniritsidwa. Ndipo Mawu akankhidwira kunjja, Iye angadzizindikiritse Yekha bwanji ndi chinachake chonga chimenecho?

¹¹² Ife tikuyenera kutenga Uthenga wonse, wathunthu. Ife tikuyenera. Ndipo tsopano, pokhala kuti tadzizindikiritisa tokha ngati anthu a Uthenga wathunthu, tiyeni tiwumbe khalidwe lathu. Ife tikuitanidwa kuti tiwumbidwe mu chifaniziro Chake, kuti ife tizikhoza kunyezimiritsa Kukhalapo Kwake. “Ndipo ntchito zimene Ine ndikuchita, inunso mudzazichita. Moyo umene Ine ndikukhala, inunso mudzawukhala.” Ife tikuyitanidwa, ndi Mulungu, kuti timutenge Iye ngati Chitsanzo, ndi kulola kuti khalidwe lathu liwumbidwe monga Lake. Ndi chinthu chotani! Mai!

¹¹³ Ndiyeno, pamene ife tilola khalidwe Lake kukhala mwa ife, ndiye ife timadzakhala ana, pokhala ndi malingaliro a Khristu, malingaliro, omwe ali khalidwe Lake. Malingaliro anu amapanga khalidwe lanu. “Mulole malingaliro,” Paulo anati, “a Khristu, malingaliro awa amene anali mwa Khristu, akhale mwa inu.” Mulole malingaliro amenewo a Khristu akhale mwa inu. Iwo amawumba khalidwe la mwana wa Mulungu. Tsopano, bwanji. . .

¹¹⁴ Mungomvetsera kwa miniti yokha. Ife tingakhale bwanji ndi lingaliro la Khristu limene linali mwa Iye, ndipo kenako nkumakana zinthu zimene Iye anatituma ife kuti tizichita? Ife tingathe bwanji kukaziyika zozizwitsa mu nthawi ya mmbuyo, pamene Khristu yemweyo Mwiniwake anali Mulungu, ndipo Mulungu mwa inu. Mu Kukhalapo kwa Mulungu, nthawizonse mumakhala zozizwitsa. Iye anati, “Inu mumanditchulirani Ine kuti ‘Ambuye,’ ndipo osamachita zinthu zimene Ine ndakulamulirani inu kuti muchite, zimene Ndinaziyika kuti inu muzichita?” Kodi inu simukuwona kumene ife tafika, kumene mpingo ukutsetserekeru? Ndipo ine ndimazipeza izo mochuluka kwambiri pakati pa Achipentekoste athu, nawonso. Ife tikutsetselekeru kutali kwambiri ndi Mzere wa moyo umenewo. Ife tikuyenera kubwerera ku zimenezo, mzanga, kubwereranso, chifukwa ife tikukula tsopano.

¹¹⁵ Ine ndikuwona pamene pepala la Amuna Amalonda liri lalikulu kwambiri, mochuluka mwinamwake monga limene Oral Roberts ali nalo. Ndipo ndapeza kuti pamene ife tifika pokhala aakulu, kenako ife timayamba kuchita modzikuza, mwaona, basi monga Israeli anachitira. Ndipo ife timayamba kumachita ngati tikuzifanizira ndi—ena onsewo. Kumbukirani, “Inu ndi anthu osiyana. Inu ndi fuko loyera, unsembe wachifumu, anthu achirendo.” Bwanji, ife Achipentekoste tinafika potero ife sitiri achirendonso kuposa dziko lonse. Ife timangovala, timachita, timayankhula, timapita kumakapanga zinthu zimene iwo

amachita; kuthamangira kunyumba, kukawonera televizioni, mmalo mokhala ku tchalitchi; ndi zinthu zomwezo basi zimene iwo amachita, zomwezo. Ife tikuyesetsa kumapikisana, kumayesetsa kukhala monga a Joneses. Mukuona? Ife sitikufuna kuti tizichita zimenezo.

116 Ife tikufuna kumakhala, kulipanga Baibulo ili kukhala kalilole wathu woziyang'anirapo, ndi kudzilola tokha kuwumbidwa ndi khalidwe Lake; kukhala ndi khalidwe Lake, malingaliro Ake, kulola malingaliro amene anali mwa Khristu kukhala mwa ife. Malingaliro ake nthawizonse amakhala. . .

117 Kodi malingaliro Ake anali akuti achite chiyani, malingaliro amene anali mwa Khristu? Nthawizonse kuti akhale ndi Mawu a Atate. Zinalibe kanthu zomwe zinkawonekera zonyezimira, ndi zomwe zinkawonekera mwanjira *iyi*, izo sizinkapanga kusiyana kulikonse kwa Iye. Mawu a Atate ndi omwe ankawerengeredwa. Kulikonseko, pamene Iye anakumana ndi mdierekezi, Iye sanagwiritse ntchito nkomwe mphamvu Yake kuti amugonjetse iye. Iye anagwiritsa ntchito Mawu, chifukwa ameneyo anali Iye.

118 Kodi munayamba mwaganizapo? Iye sanalembe konse bukhu pamene Iye anali pa dziko lapansi. Monga momwe ife tikudziwira, Iye sanalembe konse koma nthawi imodzi. Izo zinali pa mchenga. Kenako anazifufuta izo, mwinamwake, patsogolo pake. Nchifukwa chiyani Iye sanalembe mawu? Chifukwa Iye anali Mawu. Mukuona? Iye ankakhala Mawu. Ife sitikusowa mabukhu ochuluka kwambiri, pamene inu mukhala kalata yolembidwa ya Mulungu. Mukuwona? Mukuwona? Icho ndi chimene Mulungu akufuna kuti inu mukhale, zifanizo za Iye.

119 Inu mukudziwa, mu dziko la achikunja, momwe achikunja amayikira fano ndipo amadzizwetsera iwoeni pamaso pa fanolo, ndipo amadziyika okha mu kutengeka koteroko mpaka iwo amakhulupirira kuti iwo akhoza kulimva fanolo likuyankhula mowayankha iwo. Ndi chochitika cha mmalingaliro, koma mosiyana bwanji ndi Choonadi cha Mulungu.

120 Mulungu akukufunani inu. Iye sakufuna fano. Inu ndinu chifanizo chamoyo cha Mulungu. Ndipo inu mumadzilambatitsira nokha pamaso pa Mulungu, ndipo Iye amakudzazani ndi Iyemwini, ndipo inu mumamufotokozera Iye monga galasi loyang'anirapo, Mpingo Wake.

121 Ndi zosiyana bwanji ndi zimene ife tiri nazo. Ife timafuna kuti tikhale monga a Presbateria, Methodisti, ndi kukhala apamwamba basi. Ndipo chirichonse chiyenera kukhala chopukutidwa ndi chapamwamba. Ndipo ife tikungofika pokhala oyipa basi. Mukuwona? Mukuwona? Ife tiri ndi a . . . tikuchoka pa njira yopunthidwa imeneyo. Bwereraninso, mpingo. Ndine wachangu pa inu, chifukwa Kudza kwa Ambuye kwayandikira. Muloleni Iye akhale chifaniziro chanu

chowonetseredwa, akudziwonetsera Yekha mwa inu, chifukwa Iye nthawizonse anali akuchita ndendende Mawu a Mulungu.

¹²² Ndicho chimene aneneri ankachita, aliyenseyo. “Mawu a Ambuye ankabwera kwa aneneri.” Ndipo umo ndi momwe iwo ankadziwira kuti iwo anali. Mose, Mawu a Ambuye anadza kwa Mose. Zochuluka... Mawu a Ambuye anadza kwa Nowa. Mawu a Ambuye anadza kwa Daniele. Mawu a Ambuye anadziwonetsera Okha kupyolera mwa ana Achihebri. Icho chinali chiyani? Pamene anthu, a m’badwo uliwonse, ankawatenga Mawu a Mulungu, ndiye Mulungu ankawonetsera Mawu amenewo kwa iwo.

¹²³ Nowa anali chifaniziro ndi chizindikiro cha chiweruzo cha Mulungu chimene chinkabwera, ndipo iye anawonetsera Mawu. Ndipo pokhala ndi Mawu, Mawu omwewo amene iye anawawonetsera, anatsutsa dziko lapansi ndipo anapulumutsa nyumba yake yomwe.

¹²⁴ Daniele anali atalinga mumtima mwake, iye anali woti sadzidetsa yekha ndi dziko lapansi. Ndipo kodi izo zinachita chiyani? Izo zinapulumutsa moyo wake. Ana Achihebri, mwanjira yomweyo.

¹²⁵ Ndipo munthu aliyense amene anayamba watumikirapo Mulungu, anadzakhala chifanizo cha Mulungu, anali Mulungu akuwonetsera Mawu Ake omwe kudzera mwa iwo. Chifukwa, ana Achihebri anati, “Mulungu wathu ndi wokhosa kutipulumutsa ife.” Iwo analibe vumbulutso la izo, zosaposa zimenezo. “Koma,” anati, “komabe, ife sitigwadira fano lanu.” Icho chinali chiyani? Iwo ankawonetsera chikhulupiriro chawo mu Mawu a Mulungu. Ndipo Mulungu ankadziwonetsersano Yekha ndi kumadzinyezimiritsa, ndipo Iye anali Munthu wachinayi amene iwo anamuwona, mu kalilole ameneyo umo. Mulungu, akudziwonetsera Yekha kudzera mu mafano Ake amoyo! Oh, mai!

¹²⁶ Tsopano tiyeni tiyang’ane mu—mu kalilole wa Mulungu, Mawu, ndipo tizindikire khalidwe lathu la pano. Tsopano, ine ndikhoza kukutsinani inu pang’ono pokha.

¹²⁷ Ine sinditenga nthawi yochulukirapo. Oh, mai! Sindimadziwa kuti nthawi yatha chomwechi, kotala pambuyo pake. Ine ndiribe koloko pano.

¹²⁸ Ine ndinayang’ana pa ina usiku watha, ndipo ndinalalikira pafupifupi maora awiri. Ndinaganiza, “Mai, iyo ndi seveni koloko chabe. Ine ndikuchita bwino, ndikungoyamba kutenthedwa.” Ndipo apa inali hafu pasiti naini, nthawi yoti ndiyime.

¹²⁹ Zindikirani. Ife sitikhala nthawi yayitali, chonchobe. Ndiroleni ine ndingopereka ichi kwa inu pompano, taonani... [M’bale akuti, “Lalikiranibe.”—Mkonzi]. Zindikirani. Zikomo inu. Inu mukudziwa, pamene... .

130 Tiyeni tiwone ngati tingadzizindikiritse tokha. Tsopano mvetserani. Mvetserani ichi mwatcheru, chomwe ndikunena tsopano, khalidwe lathu lapano. Ine ndizipita pang'onopang'ono kwenikweni. Ine ndikufuna izo zilowerere mwakuya kwenikweni tsopano, ife tisanatseke. Ngati inu mukanakhala m'masiku a Nowa . . . Tsopano, tangoganizani chimene inu muli. Mukhale owona mtima ndi inueni. Chifukwa, ngati simukhala owonamtima ndi inueni, inu simungakhale owonamtima ndi Mulungu.

131 Ngati inu mukanakhala m'masiku a Nowa, ndipo nkumakhala mu khalidwe lanu lapano, inu mukanazindikiritsidwa ndi gulu liti? Tsopano taganizani za zimenezo. Gulu liti?

132 Pamene, apa pali wotentheka wachikulire atayima pamwamba pa phiri apo, izo zatsimikiziridwa, mobwereza ndi mobwereza, kwa zaka handiredede ndi twente, kuti iye wapenga, chifukwa iye akulosea mwamtheradi kuti kuli madzi amene akubwera kuchokera kumwamba uko. Ndipo zida zawo zonse zasayansi zimatsimikizira kuti iyo kunalibeko kumeneko. Ndipo chifukwa chokuti izo sizinagwirizane ndi zinthu zawo zasayansi, kodi Mulungu Wamphamvuzonse akanachita bwanji chinachake chimene chinali chotsutsana ndi malingaliro awo omwe? Mukuwona? Ndipo munthuyo anakambidwa. Iye anali choseketsa cha nthawiyo.

133 Tsopano, ine ndikudabwa. Eya. Kungofunsa zimenezo, inu mukanazindikiritsidwa ndi gulu litji? Ndi lingaliro lotchuka la tsikulo?

134 Oh, inu mukuti, "Ine—ine ndine wa tchalitchi." Izo si zimene ine ndikuzikamba. Iwo anali ndi magulu a mipingo ochuluka mu tsiku limenelo, mwinamwake kuposa amene iwo ali nawo tsopano.

135 Koma panali winawake amene anali ndi—uthenga wochokera kwa Mulungu. Uko nkulondola. Ndipo umenewo unali wosatchuka kwambiri. Gulu lake linali losatchuka kwambiri, chifukwa iye ankatengedwa ngati wotengeka. Kodi mungakhale okonzeka kudzizindikiritisa nokha ndi gulu lotengeka limenelo?

136 Njira yokhayo imene inu mukanachitira izo, ikanakhala kuti Ichu panokha chiwululidwe kwa inu. Ndipo kodi inu mumadziwa kuti iyo ndi njira yokhayo imene Mulungu anamangira Mpingo Wake?

137 Tayang'anani m'munda wa Edeni, kodi Abele anadziwa bwanji kuti iwo anali magari m'malo mwa apulo? Oh! Mukuwona? Ichu chinawululidwa mwauzimu.

138 Ndipo, taonani, pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, nthawi yodziwika kwambiri imeneyo imene Iye

ankayankhula, “Kodi anthu amati Ine Mwana wa munthu ndine ndani?”

“Ena a iwo amati, bwanji, Inu ndi ‘Mose,’ kapena Ndinu ‘Yeremiya,’ kapena ‘mmodzi wa aneneri.’”

¹³⁹ Iye anati, “Koma ine ndi—ine ndikubwera molunjika ku mfundoyo. Inu mukuganiza chiyani za Izo? Mukuwona? Osati chimene winawake akunena tsopano, koma ine ndikufuna kuti ndidziwe chimene inu mukuganiza za Izo?”

¹⁴⁰ Ndipo pamenepo pamene Petro anayankhula ndipo anati, “Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

Tsopano penyani momwe Iye anabwerezera izo.

¹⁴¹ Tsopano, ife tikudziwa kuti mpingo wa Katolika, osati kuvulaza kumverera kwa inu Akatolika, koma inu mumati Iye anamanga iwo pa Petro, pokhala thanthwe laling’ono. “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wangwa. Zipata za gehena sizingathe kuwulaka Iwo.” Mukuwona? Tsopano, ngati izo ziri chomwecho, ndiye kuti mpingo unabwerera mmbuyo. Mukuwona? Tsopano, ndiye, ngati izo zinali chomwecho, iwo unamangidwa pa munthu.

¹⁴² Tsopano, Achiprotestanti amati Iye anamanga iwo pa Iyemwini, amene anali Mwalawapangodya Waukulu, Thanthwe. Ndipo, izo, izo ziri ndi Choonadi chochuluka kwa izo.

¹⁴³ Koma mungondirola ine ndiponyeremo chinachake mu zimenezo, kungo—kungozimangitsa izo pang’ono. Ine sindigwirizana nawo awiri onsewo, ponena izi, kuti sizinali kuti Iye ankayankhula za Iyemwini, molunjika, koma mwanjira ina Iye ankayankhula za Iyemwini. Ndipo Iye sanamuphatikizireponso Petro kuposa kuvomereza kwake kwa izo.

¹⁴⁴ Chifukwa, taonani zimene Iye ananena, “Wodala ndi iwe, Simoni, mwana wa Yonasi, pakuti thupi ndi mwazi sizinakuwululire izi kwa iwe. Iwe sunaphunzire izi mwa chokuchitikira china cha ku seminare, kapena kuti winawake anakuwuza iwe za izo. Koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula ichi kwa iwe.”

¹⁴⁵ Ndiye, ndi vumbulutso lauzimu la Yemwe Yesu Khristu ali. Ndizo ndendende. Ndipo Iye anati, “Pa thanthwe ili, pa vumbulutso lauzimu, Ine ndidzamangapo Mpingo Wangwa.” Izo zinawonetsera kuti zipata zonse za ku gehena zikanadzakhala zotsutsana ndi iwo, koma izo sizidzagonjetsa iwo. Mukuwona? “Ine ndidzamanga Mpingo Wangwa, ndipo zipata za gehena sizidzatha kuwulaka Mpingo uwu.”

¹⁴⁶ Koteru, inu mukuwona, Nowa anali ndi vumbulutso lauzimu. Mulungu anali atayankhula ndi iye mwachindunji. Abele . . .

¹⁴⁷ Pamene Kaini anapereka zipatso za mmunda, monga ma apulo ndi zipatso, ndi zina zotero, ndi kulipanga guwa lake

kukhala lokongola, ndipo anati, “Mulungu avomereza izi chifukwa ine ndachita *izi*, ndipo anakonza maguwa aakulu. Ndipo ine ndalikongoletsa. Ndalipanga ilo kukhala lokongola. Ife tiri ndi tchalitchi chachikulu kwambiri mu mzindawu, kapena zina zotero. Mulungu adzavomereza izo, mu *izi*.” Iye samalandira ntchito ya manja a munthu aliyense, mu chiwombolo.

¹⁴⁸ Koma Abele anabweretsa mwanawankhosa ndipo anapereka magazi, ndipo Mulungu anachitira umboni kuti iye anali wolungama. Kodi iye anadziwa motani izo? Kunalibe Mawu olembedwa mmasiku amenewo. Ilo linali vumbulutso, ndipo momwemonso izo ziri chomwecho lero.

¹⁴⁹ Inu mukuti, “Chabwino, ndine wa tchalitchi. Mpingo wanga ndi wabwino basi monga mpingo wanu. Iwiri yonseyo ndi yopangidwa ndi nyumba ya mtundu wofanana, zipangizo za mtundu wofanana.” Uko nkulondola. Nyumbayo ilibe kanthu kochita ndi zimenezo.

¹⁵⁰ Bungwe ndi gulu la anthu amene amasonkhana pamodzi, ndikupanga malamulo a zomwe iwo amaima nazo, ndipo ndi zimenezo. Palibe chotsutsa izo, izo zonse ziri bwino, koma izo si zomwe ine ndikuzikamba. Inu mumavala zovala za mtundu womwewo, mwinamwake, ngati izo ziri zaukhondo, zomwe okhulupirira ena akanakhoza kuchita, ndipo komabe izo sizimapanga izo.

¹⁵¹ Koma tsopano tayang’anani apa. Chimene icho chiri, ndi vumbulutso lauzimu la Mawu a Mulungu. Kutu, china chirichonse ndi cholakwika koma Mawu amenewo, ndipo inu muwakhulupirire Iwo. Iye anali Mawu, ndipo Iye ndi Mawu, ndipo Iye nthawizonse adzakhala Mawu. Ndipo pamene Mulungu angatsegule mpita umenewo, ndiye Iye akhoza kuyenderera momasuka kupyola mu thupi loyeretsedwalo.

¹⁵² Tsopano, tsopano, tsopano ife tikuzindikira kuti ngati inu mukanakhala mu tsiku limenelo, ndi gulu liti limene inu mukanadzindikiritsidwa nalo; ndi mneneriyo, ndi Mawu otsimikiziridwa, ngakhale iwo anali ochepa? Kapena, kodi mukanakhala ndi anthu a lingaliro lotchukawo? “Chabwino, ine ndikukuwuzani inu, ine ndikukhulupirira kuti munthuyo wapenga.” Ndipo njira yokhayo imene mukanadziwira kuti sanali wopenga ndi kuti Mulungu yemweyo awululire kwa inu chinthu chomwecho chimene Iye anawulula kwa Mose.

¹⁵³ Ndipo njira yokhayo imene ife titi tidzathe kukhalira konse zifanizo za Mulungu, ndi ana a Mulungu, ndi kuti Mulungu awulule kwa ife, ndi kudziwonetsera Yekha kupyolera mu Mawu Ake, kwa ife, ndi ife ku dziko lapansi. Ndiwo mpita wokhawo. Pakuti, Khristu anali Chifanizo pano pa dziko lapansi, chimene munakhoza kuchiwona, Mulungu mwa Munthu, Chifaniziro chofotokozedwa cha Mulungu, chifukwa Mulungu anali mwa

Iye mochulukwa kwambiri mwakuti iwo anali Mmodzi. Ndipo tsopano pamene Khristu anachoka, Iye anawuyetsa Mpingo, kuti Mpingowo udzakhoze kutenga malo Ake ndi kuwonetsera Mawu a Mulungu. Mukuwona? Imeneyo ndi njira yokhayo imene izo zingachitikire. Oh, mai!

¹⁵⁴ Kodi makanakhala ndi anthu otchukawo amene anali ndi lingaliro lotchuka? “Bola ngati ine ndiri wa mpingo!” Ndipo mwinamwake, “Chifukwa ine ndinavina mu Mzimu, ine ndiri bwino.” Mwinamwake, “Chifukwa ine ndinayankhula ndi malirime, ine ndiri bwino.” Kapena mwinamwake, “Ife tiri ndi abusa abwino, ndipo ine ndiri bwino.” Tsopano, zinthu zimenezo ndi zolemekezeka. Ine ndiribe kanthu koti ndinene motsutsa izo. Izo nzoona.

¹⁵⁵ Koma dongosolo ili la chipulumutso ndi chokuchitikira munthu pawekha. Kuyankhula mmalirime ndi mphatso ya Mulungu. Kuvina mu Mzimu ndi Kukhalapo ndi Ulemelero wa Mulungu. Koma inu kulola khalidwe lanu liwumbidwe mu chifaniziro cha Mulungu, kuti Iye azidziwonetsera Iyemwini, ndipo inu ndi—ndipo inu nkukhala fano Lake, likuyenda pa dziko lapansi, chifaniziro chowonetseredwa cha Iye.

¹⁵⁶ Tsopano, kodi makanakhala ololera kuchita zimenezo m’masiku a Nowa? Kapena makanakhala kumbali yotsutsa, kutsutsa ziwiri zonse mneneriyo ndi uthenga wake wotumizidwa ndi Mulungu? Tsopano taganizani za zimenezo. Ndi mbali iti imene inu makanaganizira, momwe muliri tsopano, imene makanaitenga? Tsopano mukhale owonamtima. [M’bale Branham akukhosomola—Mkonzi]. (Mundikhululukire ine.) Palibe chifukwa choti ine ndiziyesetsa kunena izo. Inu, inu mukuyenera kuziganizira izo, inueni.

¹⁵⁷ Kapena mmasiku a Eliya, pamene iye anayankhula mokwanira za nkhope zopenta, ndi—ndi dona wamakono wa oralo, Yezebeli ameneyo, atakhala pamenepo akutembenuza wake—mutu wa mwamuna wake mwanjira iliyonse imene iwo unkafuna kupitako? Ndipo kaya iwo unkafuna kapena ayi, iye ankawutembenezira iwo, mulimonse. Ndipo alaliki onse akugwirizana nazo, “Izo zonse ziri bwino. Mwaona, izo zonse ziri bwino, chifukwa mfumukazi yathu!” Mukuwona? Ndipo iwo onse mophweka anagwera mu chochitika chimenecho.

¹⁵⁸ Ngati icho sichiri chithunzi cha lero, ine sindinawonapo izo. Zinthu zopusa zonsezi zimene anthu akuchita, ndipo, komabe, mu Dzina la Khristu. Ngati Iye anali wolakwa pa zonsezo? Iye siwolakwa pa chirichonse cha izo. Inu mukudziwa bwanji kumene Iye. . . .

Mawu amafotokoza izo. Tiyeni tingotsatira mmusi maminiti pang’ono ndi kuwona.

¹⁵⁹ Kodi inu makanakhala ku mbali yotsutsayo? Kodi inu makanakhala kumusi uko ndi Eliya, mutayima kumeneko

pamene Eliya ankawoneka kuti anali yekhayekha, ndipo aliyense kumaganiza kuti iye anali chothimbirira chachikale kapena chinachake? Koma izo sizinamuvutitse iye ngakhale pang'ono. Iye anali ndi Mawu. Ndipo iye anali ndi Mawu, ndipo iye samachita mantha ndi Mawu. Iye samachita mantha, ndi Iwo. Munthu aliyense amene ali ndi Uthenga wa Mulungu samawopa kalikonse. Uko nkulondola.

¹⁶⁰ Stefano wamng'ono anaimirira m'mawa umenewo pamaso pa Sanhedrini, iye anati, “Bwanji, inu owuma-makosi, osadulidwa mu mtima ndi mmakutu, inu nthawizonse mumawukaniza Mzimu Woyera. Monga makolo anu ankachitira, inunso mukutero.”

¹⁶¹ Baibulo linati, “Nkhope yake inkawoneka ngati ya Mngelo.” Ine sindimakhulupirira, izo monga kuwala kwamagetsi kapena chinachake. Mngelo amadziwa pamene iye wayima. Mngelo samawopa kalikonse. Iye ndi Mtumiki wochokera kwa Mulungu.

¹⁶² Ndipo munthu aliyense amene ali ndi Uthenga wa Mulungu amadziwa pamene iye wayima. Iye samasamala za aliyense, chimene iwo akufuna kunena pa Iwo. Sipamakhala mabishopu kapena china chirichonse chimene chimamukankhira iye pamenepo. Iye amadziwa ndendende pamene iye wayima, ndipo izo zimakhazikitsa icho. Mulungu amatsimikizira Uthenga wake ndipo amatsimikizira kuti Iwo ndi woona, kotero iye amayima ndi Iwo. Iye samakhala ndi mantha. Icho ndi chifaniziro chowoneteredwa cha Mulungu.

¹⁶³ Icho ndi chimene Yesu anachita. Iye sanachite mantha kunena kuti, “Oh, Afarisi akhungu inu, ndinu—ndinu amene mumamanga manda a aneneri, ndipo ndinu amene munawayika iwo mmenemo. Inu ndinu wa atate anu, mdierekezi,” ndipo ma akibishopu ndi china chirichonse. Iye sankachita mantha, chifukwa Iye ankadziwa pamene Iye anali. Inde.

Mmasiku a Eliya, kodi inu mukanatenga mbali iti?

¹⁶⁴ Kapena, mmasiku a Mose, pamene kunali Uthenga wa Mulungu, wotsimikiziridwa bwinobwino, tsopano mveterani, mu chikhalidwe chanu cha pano (Mukuti, “Ine ndine Mkhristu.” Chabwino.), Ine ndingokufunsani inu: Khalidwe lanu lapanoli, inu mukanatenga kayimidwe kotani? Pamene, Datani anadzuka ndipo anati, “Tsopano dikirani miniti yokha. Alipo amuna oyer ambiri kuzungulira kuno pambali pa iwe, Mose. Tikangotenga gulu la amuna ndi kudzatipangira ife chochitika chachikulu kuno. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, ife tidzakhala ndi mabishopu ndi maakibishopu, ndi china chirichonse, kuzungulira kuno. Ndipo Mulungu amakhala mwa anthu Ake, chinthu chonsecho. Usamaganize kuti ndiwe nsangalabwi yokhayo mmphepete mwa nyanjayi.” Pamene, Datani anayima pamenepo, anati, “Kodi anthu inu simukuganiza zimenezo? Munthu ameneyo akudzitengera

zochuluka m’manja mwake momwe. Iye akuyesetsa, kutiwuza ife zoti tizichita. Bwanji, mu unyinji wa—wa ambiri mumakhala uphungu, mumakhala—mumakhala chitetezero. Bwanji, ife tonse tikuyenera kusonkhana pamodzi ndi kukonza chinthu ichi.” Koma panali Uthenga wa Mulungu, anatsimikizira Uthenga wake.

¹⁶⁵ Ife sitikusowa kuti tizimufunsa winawake chinachake chokhudza Uthenga uwu umene ife tikulalikira. Iwo unalembedwa umu mu Baibulo, ndipo Mulungu amatsimikizira kuti Iwo ndi woona. Kotero nchifukwa chiyani inu mukuyenera kumatuluka ndi kukati, “Tsopano, inu Akatolika, kodi ife tichite chiyani za *ichi*? Ife tijowina a—Chitaganya cha Mipingo. Ife tifufuza zimenezo. Ife tisonkhana pamodzi ndi abale amenewo ndi kuwona momwe iwo anamangira magulu awo aakulu.” Ife anthu achipentekoste sitikusowa zimenezo. Ife sitikusowa kujowina Bungwe la Mipingo Yadziko Lonse. Ife tikusowekera kujowina gulu loyimba la Kumwamba, mphamvu ya chipentekoste, kukwezedwera mmwamba kupita ku malo Ammwambamwamba. Ife sitikusowekera zinthu zimenezo.

¹⁶⁶ Koma, inu mukuwona, ndi mbali iti yomwe inu mukanatenga, mu khalidwe lanu lapano, ngati Datani akanadzuka ndi kunena zimenezo, ndipo inu mukanakhala mutayima pamenepo pa nthawi imeneyo? Kodi inu mukanagwiritsa ku uthenga wa Mulungu ndi mtumiki, ndi kukhala ndi izo, ndipo utatsimikiziridwa bwinobwino kuti ndi Choonadi? Kapena, inu mukanatenga anu—mapepala anu ndi kupita ndi kukajowina gulu lina? Oh, izo ndi... mwaona, tangoganizani za zimenezo.

¹⁶⁷ Pamene izo zinkawoneka kuti zonse zinali zotsutsana ndi Uthenga wotsimikiziridwa wa Mulungu ndi mtumiki wa m’badwo umenewo, zinthu zinafika povuta kwa Mose. Chirichonse chinali chitapita, zinkawoneka ngati Mulungu anali atamusiya iye. Koma iwo anali atamuwona kale Mulungu akuchita chinachake. Iwo ankadziwa kuti Mulungu anali mu izo.

¹⁶⁸ Tsopano, kapena, mmasiku a Khristu...Ife tifulumira. Mmasiku a Khristu, inu mukanatenga mbali iti, pamene mipingo yonse yayikulu ndi azaumulungu awo amakono ndi aphunzitsi ankamutsutsa Iye ndi mfundo Zake, ndi Kuphunzitsa Malemba komveka bwino? Iwo ankatsutsa Iwo. Pamene mpingo wanu umene inu munkapitako ukanati, “Munthu ameneyo ndi wotengeka. Chabwino, iye sanachokere konse ku seminare yathu. Ife tiribe mbiri ya iye akupita ku sukulu zathu. Iye alibe khadi yachiyanjano. Iye samanyamula zomuyenereza. Kotero, mnyamatayo ndi wopenga. Musakhale ndi chochita ndi izo,” kodi inu mukanachita chiyani mu chikhalidwe chanu chapano? Mungofunsa izo kwa miniti. Chabwino. Kodi inu mukanachita chiyani? Ngati Iye... .

169 Ngati inu mukanakhala moyo mu tsiku limenelo, ndi kukhala wa ku—a—Sanhedrini, ndipo izo ndi ngati—Bungwe la Mipingo Yadziko Lonse. Ndipo mpingo wanu unalowa mu mgwirizano umenewo, ndipo iwo akanatenga zinthu zonsezi. Ndipo Munthu uyu anadzuka, ndipo inu munamuwona Iye akuchita ntchito za Mulungu, ndipo palibe amene akanakhoza kumutsutsa Iye. Komabe, Iye nkumaganiziridwa kuti “Munthu wopenga, wobalalika mmutu Mwake.” Iye anali a . . .

170 Mulungu andikhululukire ine chifukwa cha kufotokoza uku, koma Iye anali mmodzi wa “zosamvetsetseka” za tsiku limenelo. Mwaona, ine ndikuzipanga izo kuti inu mumvetsetse.

171 Chifukwa chiyani? Iye anali wobadwa wa Kumwamba. Khalidwe lake linali la Kumwamba. Ilo silina—silinayanjane ndi mgwirizano wa zitaganya za dziko lino. Mukuona? Iye sanali munthu wa mtundu umenewo. Ilo likanayima kuti pamene afioloje onse, aphunzitsi onse, amati, “Kodi Munthu uyu anachokera kuti? Ife sitikudziwa nkomwe kumene Iye anachokera?”

172 Pamene Iye anachiritsa munthu wakhunguyo, iwo anati, “Bwanji, ife sitikudziwa kumene Munthu uyu anachokera. Perekani ulemelero kwa Mulungu. Ife sitikudziwa chirichonse cha Munthu uyu. Kodi Iye anachokera kuti? Ife—ife tiribe zolemba za Iye. Iye sali pa ndondomeko yathu. Iye sali mu gulu lathu la oyang’anira, Iye—Iye—Iye sali paliponse. Palibe mmodzi wa iwo amene akudziwa kanthu za Iye. Kodi Iye anachokera kuti?”

173 Mwamuna wakhungu anati, “Icho ndi chinthu chodabwitsa, kuti Munthu akhoza kutsegula maso anga, ndipo komabe inu simukudziwa kumene Iye akuchokera. Ndipo inu mukuyenera kukhala atsogoleri a tsiku lino.” Eya. Anati, “Tsopano, kaya Iye ndi wochimwa kapena ayi, ine sindinganene zimenezo. Ine sindine wazafioloje. Koma chinthu chimodzi chimene ine ndikuchidziwa: kuti ndinali wakhungu, ndipo tsopano ndikupenya.” Ndi zimenezotu. Icho ndi chimene chinkafunikira. Iye ankafuna kupenya. Inde.

174 Njira, amakono onse, aphunzitsi onse a Baibulo ankamutsutsa Iye ndi Mawu Ake ocheka-owona ochokera kwa Mulungu. Inu mukukhulupirira kuti Iye anali wachikhazikitso mwamtheradi, sichoncho inu, mu kuphunzitsa Kwake? Koma osati molingana ndi masukulu awo. Kodi izo zalowelera mkati? Kodi ife tinadziwa bwanji kuti Iye anali wachikhazikitso? Iye anawafunsa iwo, “Ndani anganditsutse Ine za tchimo? Fufuzani Malemba. Iwo ndi Amene akuchitira umboni za Ine. Iwo akukuuzani inu ndendende. Tsopano, ngati Ine sindikuchita chimene Lemba likunena, ndiye Atate nkusatsimikizira izo kupyolera mwa Ine, ndiye ndiponyerani Ine kunjja;

ndikulakwitsa.” Inde, bwana. Tsopano, ife tikupeza kuti iwo ankatsutsa Iwo, Mawu owona a Mulungu.

¹⁷⁵ Oh, kodi chikhalidwe chanu chapano chingakuzindikiritsemi ndi Iye, kapena ndi gulu lochititsidwa khungu lija la Afarisi? Kodi chikhalidwe chanu chapano, kodi mungagwiritsitse ku tanu—tizikhulupiriro tanu ta mpingo wanu? Kodi inu mungagwiritsitse kwa izo chifukwa kuti abusa anu anali, mwinamwake, inu mungati, “Chabwino, iye ndi munthu wabwino”? Iye akhoza kukhala munthu wabwino ndipo nkukhalabe wakhungu. Ndithudi. Kodi Yesu sananene, “Inu atsogoleri akhungu a osapenya”?

¹⁷⁶ Tsopano, mu chikhalidwe chanu, tangoganizani tsopano, kodi inu mukanachita chiyani? Kodi inu mukuzindikiritidwa pati pakati pa khamulo kumeneko? Kodi chikhalidwe chanu chapano ndi chotani? Kodi mukanakhala ndi Mfarisi, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu, amayi anga anali a mpingo *wuwu*, ndipo iwo ndi wabwino basi monga uliwonse wa iyo. Ine ndingokhala pomwe pano”? Mukuwona?

¹⁷⁷ Ndipo pamene inu munawona Mawu a Mulungu akutsimikiziridwa, Iwo ndi Choonadi, mwa mtumiki, ndipo inu munafufuza Malemba ndipo munazidziwa Izo. Koma chanu—chipembedzo chanu chinati, “Masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu choterocho monga icho.” Tsopano, inu mukanachita chiyani mu chikhalidwe chanu chapakali pano? Ambiri a inu mwaziwonetsera izo.

¹⁷⁸ Ngati inu munganene mu mtima mwanu tsopano, “Ayi, ine sindikanakhala ndi Afarisi amenewo. Ine sindikanadzizindikiritisa ndi iwo,” ndiye nanga bwanji tsopano? Lemba limati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Nanga bwanji tsopano? Inu mukuti, “Ine sindikanazindikiritidwa ndi Afarisi amenewo.” Nanga bwanji tsopano? Inu mukudziwa, mbiriyakale ikudzibwereza yokha. Ine ndinadula chidutswa pa pepala, tsiku lina, pa izo. Afarisi a tsiku limenelo anamutsutsa Iye, chifukwa cha tsankho. Icho ndi chinthu chomwecho chimene iwo akuchita lero.

¹⁷⁹ Kumbukirani, Nikodemo ananena chinthu chomwecho. Iye anati, “Rabbi, ife tikudziwa kuti Inu ndi mphunzitsi wochokera kwa Mulungu.”

¹⁸⁰ Koma chifukwa chakuti tizikhulupiriro tawo ndi zipembedzo sizimavomereza Uthenga Wake, ndiye iwo ankamuletsa wina aliyenseyo. Iye anati, “Inu simukulowamo, inueni, ndipo mukuletsa ena kuti alowemo.” Mukuona? Ndi chikhalidwe chotani! Ndikudabwa ngati tingazizindikiritse tokha ndi chinachake chonga chimenecho?

¹⁸¹ Ngati inu mukanamutsatira Iye kuti mungowona zozizwitsa Zake, monga ambiri anachitira, ndipo inu nkumutsatira Iye lero mu mpingo, kuti mungowona zozizwitsa Zake ndi kukhala

pamenepo. Koma kuti muyike dzanja lanu pansi, kuti mulandire Mzimu Woyera, inueni, inu osachita zimenezo. Iwo osachita zimenezo. Ambiri anamutsatira Iye chifukwa cha zozizwitsa Zake basi, kuti aziwone izo. Koma pamene Iye anakhazikika pa Chiphunzitso chenicheni cha Lemba, gulu linachoka kwa Iye.

¹⁸² Pamene, iwo ankakhoza kumuwona Iye akuchiritsa odwala ndi kutsegula maso. Ndipo munthu ankakhoza kukhudza chovala Chake, ndipo Iye ankakhoza kutembenuka, kuwauza iwo zinthu zimenezo. Ndi kumuwuza Filipino ndi Nataniele, ndi onse awa, zinthu zimenezo. Bwanji, mkazi wa pa chitsime, ndi zinthu zonsezi, kuti Iye anadzizindikiritsa Yekha kuti ndi—mneneri amene Mose ankamukamba, Khristu, Mesiya. Pamene iwo analibe mneneri kwa zaka foro handirede, kenako powonekera anatulukira Yesu uyu, akutsimikizira kuti Iye anali, mwaona, kuti Iye anali Mesiya.

¹⁸³ Ambiri a iwo anali atamutsatira Iye chifukwa, gawo loyamba la utumiki Wake, Iye ankayenda kuchokera ku mpingo kupita ku mpingo. Oh, iwo anamulandira Iye mokondwera, ndipo iwo anamupatsa Iye dzanja lalikulu. “Oh, Rabbi, oh, Inu ndi munthu wamkulu!” Koma tsiku lina Iye anakhala pansi ndi Choonadi cha Mwamalemba. Ndiyeno pamene Iye anadzizindikiritsa Yekha, osati kokha ngati Mchiritsi, koma monga *wotumidwaku-chokera kwa-Mulungu*, ndi Choonadi ndi Moyo, pamene Iye anadzizindikiritsa Yekha kwa Icho, oh, Izo zinali zotsutsana ndi mwambo wawo, ngakhale kwa ambiri amene ankamutsatira Iye.

¹⁸⁴ Sevente anatembenuka ndipo anachokapo. Kodi inu mukanachita chiyani? Tsopano, taganizani za zimenezo. Pamene, Munthu amene inu munamuwona akuchita zizindikiro zomwezo za Mesiya, ndipo nkumadziwa kuti Mesiya anali akubwera, ndipo Iye anali atanenera zonsezi kuti zikanadzachitika, ngakhale kwa Yohane ndi iwo, ndipo Iye anali atadziwonetsera izo, bwinobwino, ndiyeno inu munamutsatira Iye ndipo munawona chizindikiro chachikulu cha Mesiya, kutsimikizira kuti panalibe m’modzi wa azibusawo akanakhoza kupirira nawo Uthengawo, nkomwe, ndipo kenako, zonse mwakamodzi, Iye anabwera pamenepo ndi kudzaphunzitsa chinachake chimene chinali ndendende Mawu a Mulungu, koma mosiyana ndi momwe inu munaphunzitsidwira, ndiye, kodi mukanagwira mwambo wanu? Kodi mukanapita ndi seventewo? Oh, Lemba, Mawu omveka-bwino! Kodi mukanapita ndi seventewo?

¹⁸⁵ Kapena—kapena, kodi inu mukutha kuwona tsopano chizindikiritso chanu, pamene inu mukanaima? Tsopano taganizani mozama, mowonamtima. Kodi inu mukanaima pati tsopano, ndi chikhalidwe chanu chapano? Kuti, ndi gulu liti limene inu mukanazindikiritsidwamo, kumeneko? Kapena, inu mungathe kudzizindikiritsa nokha, mwachangu tsopano, kodi mungadzizindikiritse nokha ndi zimenezo?

¹⁸⁶ Ine ndiyankhula ndi ana apa, achinyamata. Kodi ungasindikiritse wekha lero, wachinyamata, ngati wokhulupirira wodzinenera, ngati mnyamata mwini chuma, mtundu wa Elvis Presley umene umakonda zosangalatsa za dziko lapansi kuposa mmene umakondera kutsatira Khristu? Kodi iwe ungasindikiritse wekha ndi gulu lamasiku ano ili, ndipo, kunena, chabwino, monga Bambo Presley awa? Monga ine ndikudziwira, iye ndi wa Chipentekoste. Ndipo wa Chipentekoste, kuti atuluke ndi kumachita monga choncho, iye wangokhala wa Chipentekoste mwa dzina. Kwa ine, ndi Yudasi wina.

¹⁸⁷ Pat Boone ndi anthu amenewo amene amadzinenera kuti ndi achipembedzo, ndi ma gwedemula amenewo ndi kudzipotokola, ndi zonyansa za mdziko, ndiyeno nkumadzinenera Chikhristu. Bwanji, ndi chamanyazi. Izo ndi zoyipa kuposa chidakhwa. Izo ndi zoyipa kuposa—kuposa hule pa msewu. Mulungu angalemekeze hule kuposa zimenezo.

¹⁸⁸ Ernie Ford ndi iwo amaimirira usiku wonse, maphwando awa ndi chirichonse, ndi kumapitirira, ali ndi mikono itakumbatira akazi, achigololo amenewo ndi chirichonse, ndipo kenako nkutuluka ndi kudzayimba nyimbo za mu tchalitchi. Apo ndi pamene wagulitsa maufulu ako akubadwa. Iwe ungasindikiritse wekha chotani?

¹⁸⁹ Mnyamata ameneyo anali ndi a...Iye anali munthu wolemera. Iye anali ndi mwayi. Iye ali, akhoza kukhala kuti anali, Mkhristu wamalonda, nayenso. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . mpingo.

¹⁹⁰ Tsopano, wachinyamata, kodi iwe ukanachita chiyani ndi zimenezo? Pamene, iwe umayesera kumachita monga Marilyn Monroe kapena ena a iwo enawo, kapena ena a akazi monga dona woyamba wa mdziko, ndi izi apa mitundu yonse ya zosangalatsa, ndi izi za kumeta tsitsi, ndi—ndi kudzikongoletsa pa nkhope, ndi madiresi othina awa, achigololo. Ndipo—ndipo amuna inu, kumawalola iwo kuti azichita zimenezo!

¹⁹¹ Ndipo azibusa inu opanda kulimba mtima kuti muzidzudzule iwo kuchokera pa guwa, aponso! Kulondola. Huh! Uko nkulondola. Eya. Uko nkulondola. [Osonkhana akuwombera m'manja—Mkonzi]. Tsopano, miniti yokha. Mvetserani. Uko nkulondola.

¹⁹² Koma nthawi zambiri inu mumakhala ndi azibusa operekedwa ndi Mulungu amene amadzudzula izo, ndipo inu simumakhalabe mu mzere ndi Mawu. Tsopano mvetserani, ife tikuzipeza, kutenga, kupita njira ina, aponso. [Osonkhana akuwombera m'manja—Mkonzi]. Uko nkulondola. Kodi ndikuyala chiyani pamaso panu? “Oh,” kuti, “iwo...” Ine ndikudziwa bwinoko kuposa zimenezo. Ine ndadutsamo, inemwini, Phoenix, kwa zaka fifitini zapitazi, ndipo

amawonekabe chimodzimodzi monga momwe amakhallira nthawizonse, kumangoipirabe basi. Koteru musayike izo zonse pa abusa. Uh-huh. Tiyeni tingonena kuti ife tonse ndi olakwa, ndipo tiyimirire pamenepo ndi kudziyang'ana tokha mu galasi. Eya.

¹⁹³ Wachinyamata, nanga bwanji zimenezo? Iwe umakonda kuyamikira kwa anthu amenewo kuposa momwe iwe umakondera a—kuyitanidwa kumene iwe wapatsidwa, kuti uwumbe khalidwe lako mu chifaniziro cha Mwana wa Mulungu? Nanga bwanji izo? Kodi ife tingachite bwanji zimenezo? Oh, mai! Kodi ukudziwona wekha ukuzindikiritsidwa, wokonda zotchuka? Nanga bwanji. . .

¹⁹⁴ Tsopano, ine ndikubwera kunyumba moyandikira pang'ono tsopano. Nanga bwanji inu Achipentekoste amene mumadziwa kwenikweni bwinoko? Uko nkulondola. Inu mumadziwa bwinoko kuposa zimenezo. Inu mukudziwa bwinoko.

¹⁹⁵ Koteru, kumbukirani chizindikiritso chomaliza cha mnyamata mwini chuma uyu. Iye anali mu gehena, akuyang'ana mmwamba kwa munthu amene anakhala moyenera, akupempha madzi. Koma iye anali atawoloka phompho lalikulu limenelo popanda kuvomereza kuthekera kwa Mulungu kuti amubweze iye. Ndipo kumeneko iye anali, ndipo uko iye akadali usikuuno, ndipo iye nthawizonse adzakhala. Chabwino. Icho ndi chizindikiritso chake chomaliza.

¹⁹⁶ Choteru, musadzizindikiritse nokha ndi mfumukazi yodziwika bwino ya ziwerewere. Kapena, musadzizindikiritse nokha ndi mmodzi wa a Elvis Presley awa kuno a mutu wa phanke, kumapitirira kunja kuno ndi gwedemula wanu ndi kuzipotokola, ndi kumadzitcha nokha Mkhristu; kapena Pat Boone wina, chifukwa inu muli ndi gitara ndipo mukhoza kuyima ndi kuchita mopusa ndi iyo.

Mulole Khristu adzinyezimiritse Yekha mwa inu. Uko nkulondola.

¹⁹⁷ Achipentekoste, lero, akuchoka ku Mawu a Mulungu.

¹⁹⁸ Kodi mukudzizindikiritse nokha ndi gulu la Yudasi? Kumbukirani, Yudasi anayambapo, kuti aziyenda ndi Iye. Tsopano, ngati izi zingapweteke, ine sindikutanthauza kuti zipweteke, koma ndikutanthauza kutsina kwambiri. Mukuona? Eya. Yudasi anayambapo ndi phazi la kumanja. Iye anayambapo, kuyenda ndi Iye. Koma pamene iye anafika pakuti. . .kupeza ndalama pang'ono m'manja mwake! Uh-huh.

¹⁹⁹ Ine ndikudabwa ngati zimenezo zingaidwe kwa Pentekoste? Pamene ife tinachoka pakona ya msewu, ndi kuisiya mishoni yaying'ono mu ngalande, ndipo kenako ife tinafika pokhala ndi ndalama pang'ono. Ndipo ndikudabwa ngati kuyenda kwathu sikunapotoke pang'ono. Pamene ife tinapeza gulu la. . .Mwinamwake gulu la anthu limalowa mmenemo,

ndikuti, “Oh, chabwino, *ichi*,” kuyankhula za mamembala. Lero, zonse zimene inu mukufuna ndi mamembala, mamembala.

²⁰⁰ Mulungu samayang’ana pa mamembala. Iye akusaka khalidwe, kuti Iye akhoze kuyika Mawu Ake mwa winawake amene ati amukhulupirire Iye. Monga ine ndinanenera, usiku wina, Eliezara anatuluka thukuta kufikira atapeza khalidwe la mkwatibwiyo. Kenako iye anachita kumupangitsa iye kuti ayime njii, kuti amuveke iye moyenera, kuti akakomane ndi amene iwo ankamukamba. Mukuona? Bwanji, ngati mungapeze khalidwe, simungawapange iwo kuvala moyenera. Iwo sangathe. . . Umhum. Chabwino.

²⁰¹ Zindikirani tsopano, Achipentekoste amakono. Tsopano, tsopano, ife tayankhula kwa Apresbateria, Akatolika, koma ine ndiyankhula za Achipentekoste tsopano, chifukwa ife tikupita cha kuno kuti tiyimirire chinachake. Mukuona? Pentekoste, kodi icho si chinthu chachilendo, kuti, Achipentekoste mu m’badwo wamakono uno umene Baibulo linanenera kuti ukanadzakhala monga Laodikaya? Laodikaya. Pali mphunzitsi wa Chigriki wakhala apa, akundimvetsera ine. *Laodikaya* amatanthauza “mkazi.” Laodikaya ndi dzina la mkazi, mu Chigriki. Palibe mpingo uliwonse wa ina yonseyo umene ukuimiridwa ndi dzina limenelo. Koma tsopano ndi mkazi, Yezebeli. Uko nkulondola. “Ndipo ife tinalemera. Ife sitikusowa kanthu.” Koma sitikudziwa kuti ndife “amaliseche, akhungu, omvetsa chisoni,” tinachoka pa Njira. Kodi ife tachita chiyani? Ife tinatolera chuma china, mwinamwake, monga Yudasi anachitira, mwawona, ndiye ife sitinayende ndi Iwo kenanso. Kugulitsidwa, chifukwa cha phindu lina, anthu ambiri amachita zimenezo. Zipembedzo zambiri zimanyengerera pa Mawu, ndi cholinga chakuti apeze mamembala ochuluka, phindu lawokha; kuchita chirichonse.

²⁰² M’busa wina abwere mu deralo ndi kudzamanga ntchito yabwino. Ndipo zikatero iwo amakhala ndi msonkhano, msonkhano waukulu kwinakwake, ndipo iwo amamuchotsapo munthu ameneyo, ndi kumutenga mnyamata wina wamng’ono Ricky wachabechabe nkukamuyika iye kumeneko, ndipo izo zimangobalalitsa nkhosazo. Ngati Mulungu amuyika munthu mmenemo. . . Koma, oh, iwo amachita zimenezo pa misonkhano, nthawi zambiri; kumutengapo, nkumuchotsapo m’bale wina wosauka, ndipo amene anaimanga kwenikweni ntchitoyo. Kenako, iwo osadziwa kuti akuthyola khosi lawo lomwe pochita zimenezo, ndi kuwuvulaza mpingo.

²⁰³ Kugulitsidwa, ku kutchuka, malingaliro a wekha, phindu, phindu lawekha, mipingo yaikulu, zipembedzo zazikulu. “Gulu lathu ndi lalikulu kuposa lanu nonse.” Oh, imeneyo ndi njirayo. Abaptisti anali ndi mbalume, “Millioni ina mu ’44.” Koma inu mwapeza chiyani?

204 Ine ndinati, usiku wina, “Kuvomereza; miyala ndi kuvomereza.” Kodi mwala uli ndi phindu lanji popanda mmisiri wamiyala ali ndi Lupanga lakuthwa konsekonse la Mulungu, kuti awawumbe iwo ndi kuwadula iwo kukhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu? Inde.

205 Kodi Yudasi anachita chiyani? Kodi iye anachita chiyani? Kumbukirani chikhalidwe chake chomaliza. Oh, kodi iye anachita chiyani? Iye anakaikira zonena za Khristu, iye atatha kuyamba kuyenda ndi Iye. Achipentekoste, inu musamachite zimenezo. Amuna Azamalonda, inu musamachite zimenezo. Musamakayikire zonena Zake. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Yudasi anakayikira zodzinenera Zake, ndipo anadzakhala wotchuka kwambiri ndipo anagulitsa Izo. Khalidwe la Yudasi linamupangitsa iye kuti amugulitse Iye, kwa omutsutsa Ake.

206 Ndipo lero chinthu chomwecho chikuchitika. Nthawi zambiri khalidwe limene timadzilola tokha kuti tiwumbidwe nalo, limatigulitsa ife, ku zosamalira za dziko lapansi, kwa anthu amene angatitsutse. Chinthu chomwecho chimene Pentekoste inatulukamo, iyo ikubwereranso mu icho kachiwiri, basi mwachidziko pafupifupi monga iwo analiri mmalo oyambirira. Mukuona? Icho ndi chiyani? Ife timalephera kuwulola Moyo Wake kuti unyezimire mwa ife.

207 Kapena, kodi inu mukudzipeza nokha mukuzindikiritsidwa ndi ophunzira Ake owona? Ameni. Apo ndi pamene ife tikufuna kukhala, owona kwa Iye, owona ku Mawu Ake. Kukhala pamenepo, pamaso pa otsutsa! Ameni. Kodi pamenepo ndi pamene inu mukudzipeza nokha kukhala odzindikiritsidwa usikuuno? Athokozeni Ambuye. Ameni. Kulola Moyo wa Khristu uyenderere mwa iwo! Inde, bwana. Iwo anali atayeretsedwa ndi kudza Kwake. Ndipo munthu wochimwa, pa kuvomereza... Ndipo kuyeretsedwa kunali kutawayeretsa iwo, ndipo mitima yawo inali yokhazikika kwambiri kwa Mulungu mpaka Khristu anadzitsanulira Iyemwini mwa iwo ndipo ananyedzimiritsa Kukhalapo Kwake ku dziko lapansi. Pamaso pa otsutsa, iwo anayima monga Iye anachitira. Iwo anayima mowona ku Mawu, kufika pakuti wina anati, “Inu munatsala pang’ono kuti mundinyengerere ine kuti ndikhale Mkristu,” m’modzi wa ake...otsutsa.

208 Kodi inu mungadzizindikiritse nokha ndi Petro pa Tsiku la Pentekoste? Kodi mungadzizindikiritse nokha mu Machitidwe 2?

209 Pamene, anthu amati, lero, “Mzimu Woyera unaperekedwa kwa atumwi thwelovu okha.”

210 Kodi mungadzizindikiritse nokha ndi Petro, pamene iye anati, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezano

liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana”? Mzimu Woyera womwewu!

211 Kodi inu mukudzizindikiritsa nokha pamenepo ndi iye tsiku limenelo? “Ine ndikuyima ndi iwe, Petro. Inde, bwana. Pa ziphunzitsa zako zachikhazikitso cha Lemba, ine ndayima pamenepo. Ine ndikufuna moyo wanga udzinyezimiritsa Lemba, monga momwe wako unkachitira kumeneko, pamene firii sauzande analasidwa mmitima yawo.”

212 Pamene iwo anawona kulimba mtima kwa iwo, masiku angapo izo zitachitika, iwo anadziwa kuti iwo anali ali ndi Yesu. Iwo anali ndi Mawu, ndipo iwo ankadziwa kuti Mawu ankakhala moyo kudzera mwa iwo. Ndipo iwo ankachita mantha kuwasokoneza Mawu a Mulungu amenewo, chifukwa iwo anali oyimirira Mawu amenewo, ndi moyo woterowo, kuti Mulungu akanadzinyezimiritsa Iyemwini kupyolera mwa iwo.

213 Anamuwuza munthu, “Siliva ndi golide ine ndiribe. Ine ndiribe nyumba zazikulu ndi zinthu zazikulu. Chimene ine ndiri nacho, ine ndikupatsa iwe. Mu Dzina la Yesu Khristu, ima pa mapazi ako.” “Chimene ine ndiri nacho!” Iye ankayenera kukhala ndi chinachake iye asanachipereke icho. Ameni. Oh, mai!

214 Powona kuti Mawu ali omwewo kwanthawi za nthawi, m’badwo uliwonse, onse amene Mulungu awayitana adzawona chinyezimiritsa.

215 Kapena, ndi Paulo, pamene wotchuka, Demasi wokonda dziko lapansi anamusiya iye, kupita kwa Akhristu ake, otchedwa, abale a malingaliro otchuka. Pamene Paulo anayima pa Mawu, “Demasi anamusiya iye, chikondi. . .kukonda dziko lapanoli.” Anamusiya iye, chifukwa chakuti iye anali woona ku Mawu. Zinali zowongoka kwambiri kwa iye. Kodi inu mukanapita ndi ndani, Demasi, kapena mukanapita ndi Paulo? Fufuzani Mawu. Kodi inu mukanatenga mbali iti mu chikhalidwe chanu chapano pa nthawiyo? Komabe, iwo ankatchedwa Akhristu.

Paulo anati, “Anthu onse andisiya ine.” Mnyamata wosauka wamng’ono!

216 Ine nthawi zonse ndinkadabwitsidwa ndi Dr. Ern Baxter. Iye anati, “Inu mukudziwa, pamene ine ndidzafika Kumwamba, chinthu choyambirira chimene ine nditi ndidzachite?”

Ine ndinati, “Ndi chiyani icho, M’bale Ern?”

217 Iye anati, “Ine ndidzapita kwa Demasi komwe ndi kukamumenya mbama pa nkhope molimba momwe ndingathere.”

Ine ndinati, “Tsopano, Ern.”

218 Iye anati, “Ine ndidzanena, ‘Nchifukwa chiyani iwe unamusiya Paulo kumusi kumeneko monga chomwecho?”

219 Ine ndinati, “Iwe ukuganiza kwenikweni kuti iye adzakakhala Kumeneko, Ern?” Ine ndinati, “Usamale nacho chikhumbo chako chofuna kukamumenya iye mbama pa nkhope.” Ine ndinati, “Ine sindingafune kukakhala kumene iye anali, mwinamwake, mwaona, kukachita zimenezo.”

220 Monga wachikunja uja ananena, ananena kwa mtsikana wamng’onyo. Iye anati, “Iwe umalikhulupirira Baibulo limenelo?”

Anati, “Ndithudi.”

221 Anati, “Ine ndikuganiza iwe umakhulupirira nkhanu ija ya Yona, chinsomba chikumumeza Yona.”

Iye anati, “Ndithudi.”

Anati, “Iwe ungatsimikizire izo motani, mwanjira ina kupatula mwa chikhulupiriro?”

Anati, “Ndikadzafika Kumwamba, ndidzakamufunsa Yona.” Uko nkulondola.

Anati, “Nanga bwanji ngati Yona kukakhala kulibeko Kumeneko?”

222 Anati, “Ndiye iwe udzakamufunsa iye.” Kotero ine ndikuganiza kuti izo zikukhazikitsa izo. Mukuona? Inde, bwana. Iye akuyenera adzakamufunse iye. Kotero, inu mukuwona, ndiye, izo zikukhazikitsa izo.

223 Ine ndikukhulupirira, ndiye, ngati iye anamusiya Paulo ndi kuwasiya Mawu, iye anachita chinthu chomwecho chimene Yudas anachita. Inde, bwana. Kodi inu mukanatenga mbali iti, pamalo amenewo? Tsopano mvetserani, Achipentekoste. Kodi inu mukanatenga mbali iti? Ine ndakhala ndikuwakanda Achipresbateria awa, ndi ena otero, tsopano kodi inu mukanatenga chiyani? Kodi inu mungatenge mbali iti pano?

224 Kapena, ndiroleni ine ndikufunsi inu chinthu chimodzi chinanso. Ichi chikhoza kupweteka pang’ono, koma ine ndikufuna ndikufunsi inu chinachake. Pamene, nkhanu inabwera mu mpingo waku Korinto, yokhudza alaliki achikazi; ndipo iwo akudula tsitsi lawo, akazi. Ndipo nkhanu inabwera, ndipo Paulo anatenga maimidwe, kuti, “Iwo asamapangidwe kukhala alaliki.” Paulo anatenga maimidwe, kuti, “Mkazi, akameta tsitsi lake, iye amanyozetsa mwamuna wake, ndipo sakuyenera kuwonedwa nkomwe akupemphera pa gulu.” Kodi, mu kachitidwe kanu kapano, inu mukanatenga nkhanu yanji? Tsopano muyang’ane mu kalilole. Ine kulibwino ndizisiye izo zokha. Ine ndikufuna kuti inu muyang’ane pa kachitidwe kanu kapano. Ndi gawo lanji linachita . . . Lanji, kuti? Lanji, kuti? Inu mukuyang’ana pati tsopano? Inu mukuyang’ana pa chiyani?

225 Paulo ankanyezimiritsa Khristu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndithudi.

226 “Paulo,” inu mukuti, “oh,” mkazi anandiwuza ine, anati, “iye anali chabe wodana ndi akazi wakale.”

227 Paulo anati, ndipo—ndipo cha mu Agalatiya 1:8, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba abwera ndi kudzalalikirira chinthu china chirichonse kupatula ichi, kwa inu, mulole Iye akhale wotembereredwa.” Uko nkulondola. Uko nkulondola. Tsopano, chiyani . . .

228 Kodi inu mukunyedzimiritsa pati tsopano? Uh-huh. Musatenge mbali yotchukayo. Mutenge mbali ya Mawu. Uh-huh. Oh! Inde, bwana. “Anamusiya iye.”

Ndipo pamene nkhaniyo inadzabwera, bwanji, Paulo anatenga maimidwe.

Ndipo iwo analemba, anati, “Mzimu Woyera unatiuza ife kutero.”

229 Iye anati, “Chiyani? Mawu a Mulungu anatuluka mwa iwe, kapena Iwo anachokera kwa iwe wekha? Ngati munthu aliyense adziyesa yekha kukhala wauzimu kapena—kapena mneneri, iye adzavomereza kuti zinthu zimene ine ndazilemba ndi malamulo a Ambuye.” Icho chinali chiyani? Iye ankakhala ndi Mawu. Amen.

230 Tsopano, inu mukukhala pati? Izo ziri ndi inu tsopano. Inu mungopeza malo anu. Chabwino. Inde, bwana.

231 Pamenepo Paulo anayima, kwa—kwa . . . kuchoka ku malo amene iye anali nawo. Kumbukirani, Paulo, kuti achite ichi . . . Tsopano, dikirani. Ndiloleni ine ndipereke chinachakenso ife tisanachoke. Paulo, iye asanachite ichi, iye anachita kusiya udindo wapamwamba umene iye anali nawo mu mpingo wa tsiku lake, kuti akhale ndi Mawu.

232 Tsopano, ngati inu mukuyang’ana pa Paulo, nanga bwanji inu, pamene mpingo wanu ukuphunzitsa mosiyana ndi Iwo? Nanga bwanji inu, abusa, mtumiki, membala? Ndithudi.

233 Kodi iye anachita chiyani? Iye ankayenera kutenga malo awa kuchitira kuti Mbewu iyi ikhoze kukula, Mbewu ya Moyo Wamuyaya. Iye sanali wotsutsa. Iye anati, “Izo ziri ngakhale chomwecho, likutero lamulo.” Uko nkulondola. Iye sanali . . . Iye anakhala kumene ndi Mawu. Ndipo kuti achite zimenezo, iye ankayenera kuwusiya mpingo wake wa orthodox, kuti achite izi. Kuti awasunge Mawu a Moyo kuti azikula, iye ankayenera kuchita ichi.

234 Demasi ndi ena onse a iwo, anati, “Oh, inu mukhoza kungobwera. Zipitirira, Paulo, iwe ulibe . . .”

235 Koma Paulo anayima apo pomwe ndi Mawu amenewo. Wosauka wamng’ono uja, Myuda wa mphuno-yangowe, ine

ndikufuna ndidzamuwone iye Tsiku limenelo. Ine ndikufuna ndidzayime pamenepo, kudzamuwona iye atavala korona wa ofera pamene iye azidzabwera. Ine ndikufuna kudzawona pamenepo, ndikudzati, “Ulemelero! Aleluya! Paulo!” Ameni. Inde, bwana. “Kukhala pa Mawu! Ndine wokondwa, Paulo.” Koteru, ndithandizeni ine, Mulungu. Mundirole ine ndikhale pamalo omwewo. Inde, bwana. Inde.

²³⁶ Mmasomphenya amene ine ndinawawona osati kale, a anthu amenewo kumeneko, ine ndinafunsa funso. Inu munaziwerenga izo mu—mu digest, nkhani ya Amuna Azamalonda. Iwo anati . . . Chabwino, ine ndinati, “Kodi Paulo adzayenera kutero?”

Anati, “Inde, bwana.”

²³⁷ Ine ndinati, “Ine ndinayima pa Chinthu chomwecho chimene iye anachita.” Inde, bwana. Kukhalapo, chinthu chomwecho.

²³⁸ Mose anachita kuchoka pa mpando wachifumu, kuti atenge Mawu a Mulungu. Iye anasiya mpando wachifumu. Uko nkulondola. Iye anali wolowa ku mpando wachifumu. “Ndipo iye anasiya zosangalatsa zokhala Farao, pakuti anachiyesa chitonzo cha Khristu kukhala chuma chapamwamba kuposa chuma cha m’Igupto.”

²³⁹ Inu mumati, “Chabwino, ine ndikukuwuzani inu. Akazi onse adzandiseka ine. Amuna adzaganiza . . .” Ine sindikusamala zimene iwo angamaganize. Uko nkulondola.

²⁴⁰ Paulo anatsika. Mose anatsika kuchoka pampando wachifumu. Ine ndiri ndi mndandanda wa izo ndalemba apa, zikutenga masamba atatu. Koma ndiroleni ine ndikuwuzeni inu chinachake, chikuthandizani inu, mwamsanga ndithu.

²⁴¹ Yesu anatsika kuchokera Kumwamba, kuti adzazinyezimiritse Yekha mmawonekedwe a mnofu wochimwa. (Ndipo inu ndi ndani, kapena ine ndi ndani?) Kuti adzapange a . . . kudzatipangira ife njira kuti tidzanyezimiritse Mulungu, kudzapanga njira yoti adzazinyezimiritse Iyemwini mwa ife, potiyeretsera ife ku Mawu Ake. Pakuti Mawu Ake amatero, kuti, pamene Iye anatero, kuti ife tidzathe kunyedzimiritisa Mawu Ake.

²⁴² Mu Yohane 14:12, Iye anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iye adzazichitanso.” Chifukwa chiyani? Uyo anali Khristu, akunyezimiritisa. “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Komabe, inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine . . .” (“Ine,” mlowammalo wa umwini.) “. . . ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mwaona, monse mpaka kumathero a dziko lapansi.” Oh!

²⁴³ “Ngati aliyense adzanditsatira Ine, mulole iye adzikane yekha. Mulole iye akane kachikhulupiriro kake kopangidwa ndi anthu, anyamule Baibulo lake ndi kunditsatira Ine.” Uko nkulondola. Inde, bwana.

244 Zikatero, inu mukuzindikiritsidwa penapake mu Lemba. Mosakayikira, ine ndikuyenera kutseka. Inu mukudzindikiritsidwa penapake mu Lemba. Inu mukudziwa zimenezo. Aliyense wa ife, ife tikuwona kuzindikiritsidwa kwathu.

245 Mpingo, tikupita uku ku a—kusonkhana kumene kwakonzekeredwa kwa chaka. Mipingo yakhala ikupemphera. Anthu akhala akusala kudya. Ine ndatsanulira mtima wanga, kudutsa msabata yonseyi, chokwera ndi chotsika mchigwa ichi, kupita ku mng'alu wawung'ono uliwonse ndi ngodya imene ine ndikanakhoza kulowamo, kuyesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndikuchenjezeni inu za Kudza kwa Ambuye. Ndipo ndi ife apa, basi nthawi iyi isanafike apa. Ndipo tiyeni tidzizindikiritse tokha tsopano, kuti tisunthire kutsidyako, kuti tikaimirire, kapena tikamunyezimiritse Yesu Khristu.

246 Kodi tidzizindikiritsa tokha ndi kametedwe katsopano? Kodi tidzizindikiritsa tokha ndi mmene tingavalire mokongola? Kodi tidzizindikiritsa tokha ndi momwe tingayimire motchuka ndi kuyankhula, kuchuluka kwa maphunziro amene tiri nawo? Pamene, Paulo anati, zinthu zimenezo, iye ankayenera kuziyiwalala izo kuti amudziwe Khristu.

247 Kodi ife tikuzindikiritsa pentekoste? Ife tikutero? Bwanji, kodi ife tikudziweza tokha tikunyezimiritsa kuti?

248 Kodi ife tikunyezimiritsa chiyani, mulimonse, ngati ife tangokhala ndi phokoso lochuluka, ndikumakhoza kufuula ndi kuyimba, ndi kulumphu chokwera-ndi-chotsika? Oh, ine ndawawonapo Achimuhamedi akuchita zimenezo. Ndawawonapo anyani akuchita zimenezo.

249 Palibe ndemanga! Ine sindikutanthauza zimenezo, nthabwala. *Ano* si malo ochitira nthabwala. Awa ndi Mawu a Mulungu. Mukuona?

250 Koma ndawonapo nyama zikulumphu, zikusewera, akalulu. Izo sizitanthauza kanthu. Ndithudi ayi. Mumakhala osangalala. Chirichonse chimakhoza kukusangalatsani inu, kusamvetsetsa kwakung'ono kulikonse. Ine ndawawonapo ochimwa ataledzera kwambiri, ndipo atakondwa kwambiri! Ndithudi. Izo sizitanthauza kanthu.

251 Koma kodi chisangalalo chimenecho chikuchokera kuti? Gwero lake ndi chiyani? Kodi izo zikuchita chiyani pa inu? Kodi izo zikunyezimiritsa chiyani? Winawake adzakana Mawu a Mulungu; winawake adzakhala m'dziko; winawake adzamva Choonadi ndipo adzachoka kwa Icho; adzagulitsa mafulu awo akubadwa, chifukwa cha chinachake?

252 Oh, Mulungu atithandize ife, m'bale, mlongo, atithandize ife kuti tibwerere ndi kumulola Khristu kuti adzinyezimiritse Iyemwini, nayenso, mwa ife, monga chomwecho. Oh, mai! Mulungu atithandize ife kuti tizindikiritsidwe mwa Iye,

mochuluka kwambiri, kuti Mawu Ake ndi Kukhalapo Kwake zikhoze kuyenderera mwa ife, kuti adziwonetsere Yekha ku dziko, ameni, limene ife titi tidzakomane nalo.

²⁵³ Ndemanga imodzi yowonjezera, ine ndikutseka. Mvetserani mwatcheru. Wosula golide tsopano wayima mokonzeka.

²⁵⁴ Inu mukudziwa, miyala yamtengo wapatali imapezeka mu mnthaka, zida zimene timazimanya pamodzi. Koma, inu mukudziwa, ngati inu mupeza mmenemo, chinachake chitasakanizikana mmenemo, chonona chimenecho chimene munachipeza chidzasweka pakati. Unyolo sumakhala wamphamvu kwambiri kuposa polumikizira pake pofowoketsetsa.

²⁵⁵ Chotero, ngati inu mukuyesetsa kuti mukhale mwala wodulidwa kuchokera kwa Mulungu, chipangizo china, ndipo mukudzipeza kuti mukuyesera kudzipanga nokha kukhala wamkulu kwambiri, ndipo mkatikatimo inu munafinyiramo chidziko china mmenemo, mwala umenewo udzasweka. Iwo sudzapirira mayeserowo. Ndipo, mvetserani, Mulungu sadzatilandira ife, anthu Achipentekoste, pamene tibayiramo mbalume ndi china chirichonse mu Mawu a Mulungu. Iwo adza . . . Mulungu adzawukana mwalawo ndi kuwumenyera iwo ku mbali imodzi. Tiyeni tisamafunefune zinthu zazikulu.

Tiyeni tizifunafuna Khristu m'moyo mwathu. Tiyeni tizifunafuna kudzichepetsa. Mukuona?

²⁵⁶ Kumbukirani, ngati mwalawo uli waukulu, ndipo inu mukuyesetsa kuwumwaza, ndicho chimene ine ndikuwopa kuti ife tikuyesetsa kutero. Ndizo zoyankhulana ndinali nazo ndi Amuna Azamalonda awa. Zikuwoneka kuti akukula kwambiri moposa chinachake. Ndipo ine—ine . . . Ndi chifukwa chake ine ndimadana ndi . . . Ine—ine—ine ndimakonda kukhala woonamtima ndi inu, abale. Ine ndikuyenera ndidzakumane nanu kutsidyako mu Chiweruzo tsiku lina. Ndi chifukwa chimene mpingo umaganiza kuti ine ndimatsutsana ndi mpingo. Ine sinditsutsana ndi mpingo. Ndine . . .

²⁵⁷ Ine ndingadzizindikiritse ndekha pano ndi inu chifukwa chiyani? Ngati ine ndikanamaganiza kuti Abaptisti amalondola, Amethodisti amalondola, Apresbateria amalondola, ine ndikanakhala ndi iwo. Ine ndiri pano ndi inu chifukwa ine ndikudzizindikiritisa ndekha pano ndi inuyo.

²⁵⁸ Koma musamayesere kukulitsa malire anu tsopano, kukhala chinachake chimene inu simuli. Musayesere kudzipanga nokha kukhala winawake wamkulu, kumadzifanizira ndi winawake, ndi kumachita zachidziko zina mmenemo, kuti mupeze mamembala ochuluka ndi zinthu. Chinthucho chidzasweka pakati pomwe, ndipo Mulungu adzachiponyera icho pa mulu kutsidyako, kuti chidzawumbidwenso.

259 Iye adzawukitsa ana a miyala inayi, kwa Abrahamu. Uko nkulondola. Iye adzachita zimenezo. Iye adzawatenga Apresbateria, adzabweretsa chinachake kuchokera mwa iwo; Amethodisti, kapena Abaptisti. Ndipo zikuwoneka ngati Iye wayamba kuchita mwanjira imeneyo.

260 Kodi inu mukundimva ine, Amuna Amalonda? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Basi chifukwa chakuti ife tiri ndi dzina la “Pentekoste,” izo sizitanthauza kanthu kwa Mulungu. Ayi, bwana.

261 Pentekoste si bungwe. Pentekoste ndi chokuchitikira. Ndi chinyezimiritsa cha Khristu, pamene Iye anayambira pa Tsiku la Pentekoste, kuti adzinyezimiritse Yekha kudzera mwa anthu.

262 Ndipo kenako anthu anayamba kuwonjezera chidziko. Chinachitika ndi chiyani? Iwo anapita mu Bungwe la Nicaea, ndipo—ndipo anakana malonjezo omveka bwino a Mulungu, ndipo anayika mbalume mu izo. Ndipo iwo unaswa chochitika cha Chikhristu chonse mu zidutswa, ndipo iwo unapita mu Chikatolika.

263 Luther anayambitsa kukonzanso. Ndipo iye anawonetsera, ndipo icho chinaswa chinthucho kachiwiri.

264 Amethodisti anabwerapo ndi kuyeretsedwa. Ndipo iye anayamba kuwonetsera, ndipo iye anachita chinthu chomwecho.

265 Ndipo Achipentekoste akuchita chinthu chomwechonso. Oh! Chabwino, inu muyang’ane pa icho, inu mukhoza kuwona icho.

266 “Inu mumapanga bwanji...?” Mukuti, “Inu mumadziwa bwanji zinthu zimenezo?” Chabwino, ndiroleni ine ndikuwuzeni inu chinachake.

“M’bale Branham, kodi mukuloserwa?”

267 Ine sindikunenera kwenikweni. Koma pamene dokotala amupima wodwala, iye amawona zizindikiro, iye amadziwa chimene chiti chichitike. Ine ndikuwerenga kuchokera mu Bukhu la Dokotala. Ndipo ine ndikuwona zizindikiro zikugwira ntchito mu mpingo wa Chipentekoste, ndipo ine ndikudziwa kumene iwo ukulowera.

268 Siyani izo. Lekani. Bwererani. Mulungu akuthandizeni inu. Musapite njira imeneyo, anthu. Kodi inu simukuwona chimene ine ndikuyesera kuchita? Ine ndikuwotcha moyo wanga, kuyesetsa kuti ndikupulumutseni inu ku chinthu chopenga ichi chimene inu mukuthamangiramo. Tsiku ndi tsiku, chaka ndi chaka, ndimangolira ndekha. Ndipo inu mumaganiza kuti ndine mdani wanu. Ine ndi m’bale wanu. Bwererani. Musapite njira imeneyo. Kodi inu simukuwona chimene chinachitika pamene enawo anapita njira imeneyo?

269 Amuna Azamalonda, khalani kutali ndi njira imeneyo. Tsopano inu mukulemba mitundu yonse ya tizikhulupiriro m’magazini anu, ndipo izo zimakuyanjanitsani inu basi

mwachipembedzo chochuluka monga ena onsewo. Inu mukudziwa kuti izo ziri chomwecho basi. Kodi inu simukuwona kuti mukubwerera mu chinthu chimene inu mwakhala mukuchitsutsa? Tsopano, inu simundikonda ine, mwinamwake. Kulikonseko... Izo nzoona. Inu mulembe mawu anga pansi: Tembenukani, kapena inu mwapita.

²⁷⁰ Apentekoste, tembenukani, kapena inu mwapita. Bwererani ku Mawu. Ndi mochedwa kuposa momwe mukuganzira.

²⁷¹ Mulungu amafuna kunyezimiritsa, osati mamembala, koma miyala yeniyeni imene yapukutidwa ndi kuwumbidwa ndi kukonzedwa. Penyani. Wosula golide wayima usikuuno, wakonzeka kuchotsa kukayikira konse kwa zinyalala, zonse zimene zikutsutsana nanu. Ndipo mwa... Iye ali pano, wakonzeka kukuwumbani inu ndi kukupangani inu kukhala okhulupirira, kuchotsa kukayikira konse kwa inu.

²⁷² Inu kazipitani, inu mwawaona otsanzira ambiri akubwera, akuti, “*Ichi*, ndipo, ulemelero kwa Mulungu, ine ndiri ndi *ichi*. Ndipo, aleluya, ine ndiri ndi *ichi*.” Ndipo inu mumapeza kuti, iwo alibe kalikonse. Ndipo mdierekezi anachita zimenezo, kuti awutse kukaikira mu mtima mwanu. Mukuona? Iye anachita zimenezo, mwadala, kuti achite zimenezo. Koma kumbukirani, zimenezo zimangonena chinthu chimodzi, kuti, pali chenicheni chimene wotsanzira ameneyo akuyesera kuti azichita mofanana ndi icho.

²⁷³ Ulipo Mzimu Woyera weniweni. Ulipo Mzimu wa Mulungu weniweni. Ilipo mphamvu ya Mulungu yeniyeni. Alipo Mwana wa Mulungu amene akudzinyezimiritsa Yekha usikuuno monga Mzimu Woyera, kuti awonetsera Moyo Wake. Iye wayima pano usikuuno pakati panu, mmawonekedwe a Mzimu Woyera; kuti amenye ndikuchotsa litsiro lonse mwa inu, zokaikira; ndi kunyedzimiritsa kwa inu, chiwukitsitsiro Chake, kuti Iye si wakufa. Ndipo Iye ali pano kuti akuwonetseni inu kuti Iye ndi wamoyo, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye ali pano kuti adzizindikiritse Yekha ndi ife. Kodi ife sityenera ndiye kuti tidzizindikiritse tokha ndi Iye, kuti tikhulupirire Mawu Ake ndi kuwatenga Iwo?

²⁷⁴ Tiyeni tipemphere.

[M'bale akunenera—Mkonzi]. Ulemelero. Ameni. Ameni. Oh! Ameni.

²⁷⁵ O Ambuye Mulungu, momwe ife tikukuthokozerani Inu, Ambuye! Ife tinawuzidwa mu Lemba, kuti pamene Davide, pamene mdani ankaabweramo, ndipo iwo anasonkhana pamodzi, ndipo Davide ankayesera kuti awauze iwo za Mulungu, pamenepo panayima mmodzi pakati pawo, ndipo ananenera ndipo anawauza iwo choti achite, ndi momwe akanamugonjetsera mdaniyo. Zoonadi, Ambuye, ife timakhulupirira chinthu chomwecho, Mzimu wa

Mulungu umagwera pakati pathu, ndipo Mawu ndi malo oti timugonjetsere nawo mdani.

²⁷⁶ Icho ndi chimene Inu munamupatsa Adamu ndi Eva, m'munda wa Edeni, kuti amugonjetsere nacho mdani. Ndipo pamene Eva analingalira pa Iwo, ndipo nkudzawonetsera kuwalingalira Mawu, izo zinagawikana pakati, ndipo tchimo linadzalowa.

²⁷⁷ Zoonadi, Ambuye, kumeneko kwakhala kuli kugwa kwa anthu, kudutsa m'mibadwo, kuyesera kubayiramo chinachake mu Mawu. Sarah anayesera chinthu chomwecho, kuti abayire chinachake, kuti amutenge Hagara, kuti amubweretse mwanayo, koma izo zinalephereka. Nthawizonse, zakhala ziri mwanjira imeneyo, Atate. Ife—ife tikungofuna Mawu Anu, ndipo iwo okhawo; opanda chirichonse chowonjezedwa kwa Iwo, kapena kuchotsedwa kwa Iwo, basi momwe Iwo aliri. Ndipo Inu ndi Mawu awa. Ndipo ife ndi othokoza chifukwa cha zimenezo.

²⁷⁸ Adalitseni anthu pano, Ambuye. Ine tsopano, mmausiku awa pambuyo pa mausiku, ndayesetsa kunena zinthu izi, kuti Kwanu—Kwanu—Kudza Kwanu kwayandikira. Chirichonse chikulozera mwanjira imeneyo.

²⁷⁹ Ndipo kuchokera ku a—masomphenya, masabata angapo apitawo, mwanditumiza ine kuno ku Arizona. Sindikudziwa chifukwa chake. Kukhoza kukhala kubwera Kwathu kwanga. Ine sindikudziwa. Izo—izo zikuwoneka mochulukwa kwambiri mwanjira imeneyo.

²⁸⁰ Koma, Ambuye, ndiroleni ine ndimalizitse ntchito yanga. . . ndipo ndigwiritsitse Chikhulupiro, ndikusunga zovala zanga zopanda banga, Ambuye, mwa chisomo cha Khristu. Mundirole ine ndidzathe kuyima m'tsiku limenelo, ndi kudzati, "Ine ndalengeza Uphungu wonse wa Mulungu, monga ine ndimadziwira Iwo kuti ndi Choonadi, ndipo sindinapewe kunena kalikonseko." Perekani izi.

²⁸¹ Mulole abale anga, Ambuye, momwemonso, agwirizane pamodzi ndipo asunthire chifupi, ndi kudziwa kuti zilimbikitso izi—si chidzudzulo, koma ndi chenjezo, ndi kuti adziwonetsetsa mphambano. Perekani izi, Atate. Monga izo zanenedwa kumene kwa ife, kuti, Iye adzatiweruza ife ndi Mawu amenewo a Uthenga. Mulungu, ndiroleni ine ndidziyang'ane inemwini, ndipo, ine ndikuchita nazo manyazi, Ambuye, mu kalilole wa Mawu a Mulungu.

²⁸² Ine ndikumenyera, "Ndipo moona mtima, motsimikiza kumenyera Chikhulupiro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera mtima," monga Yuda ananena kuti ife tikuyenera kutero. Ndipo ife tinalonjezedwa, kuti, "Mmasiku otsiriza, Chikhulupiro ichi cha atate chikanadzabwezeretsedwa kachiwiri, ku Chikhulupiro chapachiyambi cha chipentekoste." Inu munalonjeza izo,

mu Malaki 4. Inu munati izo zikanadzachitika. Ndipo, Atate, mulole ife tikhale tikuyang'anira, ndipo athu—maso athu atatseguka, ndipo tisaphonye izo, monga momwe iwo akhala akuchitira nthawi zonse kudutsa m'mibadwo. Koma mulole maso athu akhale otseguka, kuti timuwone Yesu Khristu pamene Iye akuwonetseredwa mu ulemelero Wake pakati pa anthu Ake odzichepetsa, kuti atulutse anthu, kuchokera mwa Amitundu awa, kwa Dzina Lake. Perekani izi, Ambuye.

²⁸³ Dalitsani osonkhana awa tsopano. Ine ndayankhula motalika. Ambuye, ine sindingapepese (chifukwa, ndinamverera kuti ndinene zomwe ndinachita), powasunga iwo nthawi yaitali. Koma ndikukuthokozani Inu chifukwa cha amuna ndi akazi, lero, amene ali—akukwanitsa kumayima, ndi kudzipinda, ndi—ndi kuyesetsa kugwirizira awo—mapazi awo pansu, ndi kumamvetsera ku Uthenga. Ine ndikukuthokozani Inu chifukwa cha mipingo ngati iyi, imene ingatsegule khomo ndi kunena, “Dzaloweni mkati. Mudzatiphunzitse ife. Kapena, mudzalalikire nafe. Tithandizeni ife.” Mulungu, zikomo Inu chifukwa cha awa.

²⁸⁴ Ndipo zikomo Inu chifukwa cha kasupe, nayenso, chifukwa cha dziko lamalonda, Amuna Amalonda awa. Ambuye, mulole zovala zawo zikhale zosadetsedwa ndi zinthu za mdziko. Perekani izi. Apangeni iwo akhale malo opulumutsira miyoyo, Ambuye, amene—amene mwinamwake, kwinakwake kumene anthu samapita ku tchalitchi, iwo azidzapita kukamva anthu amalonda akuyankhula. Ndipo mulole wawo—moyo wawo ukhale wamchere kwambiri ndi chisomo cha Mulungu, ndi kudzichepetsa kwa Mzimu Wake, kuti—kuti dziko lidzalakelake kukhala anthu amtundu umenewo. Perekani izi, Ambuye. Tidalitseni ife tsopano, pamodzi.

²⁸⁵ Ambuye, tikhululukireni ife zolakwa zathu. Khululukirani machimo athu, ndipo mulole mipita ya mitima yathu itseguke. Mulole Mfumu ya Ulemelero iyende pakati pathu tsopano, ngati ife tapeza chisomo pamaso Panu, polapa zolakwa zathu. Sindikukaikira, mtima wanga walapa, mitima ina yambiri yalapa. Ndipo ngati ife tapeza chisomo, Ambuye, tiwumbeni ife tsopano.

²⁸⁶ Tsukani akachisi athu, kuti Mawu a Mulungu wamoyo akhoze kukhala pakati pathu ndi kutsimikizira kuti Yesu Khristu si wakufa. Iye si woyambitsa wakufa monga Muhamadi, kapena—kapena Buddha, kapena zina za miyambo. Iye ndi wamoyo, wanthawi yapano tsopano, Yesu wowukitsidwayo. “Iye ndi wamoyo kwanthawizonse, ndipo sangafe kenanso,” ndipo wapereka kwa ife Moyo Wamuyaya, ndipo wadziwonetsera Yekha pakati pathu. Ndipo ife, Ambuye, tikunyedzimiritisa chisomo Chake kwa ena.

²⁸⁷ Tithandizeni ife, Atate, monga Inu munalonjezera mmasiku

otsiriza chimene chikanati chidzachitike, monga zinakhalira mmasiku a Loti. Mulole ife, monga iwo amene anachokera ku Emau, tipite kwathu usikuuno, tikusangalala, chifukwa ife tikukuwonani Inu mukuchita chinachake monga iwo anakuwonerani Inu mukuchita Inu mutawuka kwa akufa; podziwa kuti chinali chinthu chomwecho chimene Inu munachichita Inu musanafe, ndiyeno iwo anadziwa kuti Inu munawukitsidwa. Perekani izi, Atate. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

²⁸⁸ Tsopano, tsopano, ine—ine ndayankhula nthawi yaitali. Koma, ichi, ine sindikudziwa kuti Iye achita ichi. Ine sindikudziwa kuti Iye atero. Ine ndingomufunsa chabe Iye. Ine ndikukhulupirira, ngati ine ndingayike moyo wanga apa kuti...pa nkhuni, kuti ndiyime ndi Mawu awa, ndiye, mwakukhoza kwa kudziwa kwanga.

²⁸⁹ Ine siwopanda tchimo. Ine ndiri nawo ochuluka akulendewera pa ine. Koma, ora lirilonse ine ndimalapa iwo, mowirikiza. Pamene ine ndiwona cholakwika changa, ndiye ine ndimachoka kwa icho, ndi kuyesetsa kuchita chimene chiri cholondola. Ine sindingayesere kupita Kumwamba pa zoyenera zanga. Ine sindingafike kumeneko. Ine mwaulemu ndikudalira mwa Yesu Khristu. Iye ndi Chidaliro changa. Ine—ine—ine ndimakhulupirira mwa Iye. Ine sindingayesere kulowamo chifukwa ndine m'bale wa Chipentekoste. Ine—ine sindingapitemo pa zoyenera za Pentekoste. Ine ndipita ndi zoyenera za Magazi a Yesu Khristu. Iye anandifera ine.

²⁹⁰ Ndipo icho ndi chimene ine ndikufuna kuti inu mudalire, zoyenera za Iye. Ndiyeno mumadziwa bwanji kuti mukupita kumeneko? Ndi pamene Mawu aliwonse alipo, inu mumavomereza Iwo ndi, “Ameni. Amen.” Chifukwa, Iwo ndi Mawu Iwoeni akuyesera kuti adzitsimikizire Okha. Ndipo ngati ife tiwakana Mawu amenewo, Iwo angakhoze bwanji kudzitsimikizira Okha?

²⁹¹ Tsopano, Yesu anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita.” Nkulondola uko? Ndiyeno kodi Iye ananena chiyani mu Yohane 5:19? “Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene awona Atate akuchita.”

²⁹² Iye anadutsa pa thamanda la Betisaida. Apo panali khamu la anthu, mwinamwake kuchulukitsa ka twente kapena ka sarte amene ali mchipinda muno usikuuno. Pali anthu foro kapena faivi handiredede, mwinamwake, amene akhala pano usikuuno. Ine sindikudziwa, koma pakhoza kukhala ochuluka chomwecho. Koma mwinamwake pali masauzande. Ndinamva kuti a “khamu” limafika ku masauzande. Tsopano, atakhala pamenepo, pali olumala, opunduka, akhungu, opinimbira, Iye anachiritisa munthu mmodzi, chifukwa Iye ankadziwa kuti

munthu ameneyo anali atakhala mwanjira imeneyo. Atate anali atamuwonetsa Iye. Mukuona? Anawasiya ena onsewo. Mukuona? Ndipo kenako Iye anafunsidwa zimenezo.

²⁹³ Koma Baibulo linanena, itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro, kuti, usikuuno, “Iye ndi Wansembe Wamkulu.” Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akanali wamoyo? [“Ameni.”] Ndipo kodi Iye ndi Wansembe Wamkulu amene angakhudzidwe ndi kumverera kwa zofooka zathu? [“Ameni.”] Chabwino, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo, malingana ndi Ahebri 13:8, ndiye Iye angachite mwanjira yomweyo. Nkulondola uko?

²⁹⁴ Tsopano tiyeni tiyeretse mitima yathu ku tchimo lonse. Tiyeni tivomereze zolakwa kwathu. Ife tivomereze kusakhulupirira kwathu, kuti ife takhala tikulakwitsa, ndi kuti, “Ambuye Yesu, apa ine ndiri. Ndine wosowa, usikuuno. Dzinyezimiritseni Nokha mmoyo wanga. Ndipatseni chikhulupiriro chimene mkazi uja anali nacho, amene anakhudza chovala Chanu.”

²⁹⁵ Ndipo ine nditi, “Ambuye Yesu, ine ndayima ndi Mawu Anu.” Kumeneko kunali kutumidwa kwanga, “Lalikira Mawu.” Ine ndayima ndi Iwo. Ine—ine ndikufuna ndife ndi Iwo. Ndipo ine nda—ine ndayima ndi kupanga zinthu zina zovuta, chifukwa cha Mawu, ndi kukhala pamene, koma Iye nthawizonse amawatsimikizira Iwo.

²⁹⁶ Tsopano ine ndikudalira pa Iye kuti awatsimikizire Mawu amenewo. Lolani iwo aponyedwe... Muloleni Iye ayenderere kupyolera mwa ife usikuuno, pamene ife tikupemphera.

²⁹⁷ Ndi angati muno akudwala, osowa, ali ndi chosowa chirichonse? Kwezani mmwamba manja anu ndi kunena, “Ndi ine, Ambuye. Ine ndikukhulupirira, Ambuye.”

²⁹⁸ Ine ndikufuna chidwi chanu chosagawanika, mokoma momwe mungathere, kwa mphindi pang’ono.

²⁹⁹ Ngati, utatha Uthenga uwu, ndipo Khristu atadzinyezimiritsa Yekha mwa anthu, ndi kuwona kuti munthu wina wosauka ali ndi chikhulupiriro chokwanira chokhudza chovala Chake, ndipo ine nkukhoza kudzipereka ndekha kwa Mzimu Wake, ndi kudziwa kuti uwu ndi Mzimu Woyera! Ndiye, ngati inu muli wa chinachake kupatula gulu lomwe limakhulupirira Izi, ndiye ndikhoza kubwera kumene iwo amakhulupirira Choonadi. Mukuona? Ine ndingatero. Ine ndithudi ndingatero. Ine ndingakhulupirire, chifukwa Mulungu akudzipangitsa Yekha kudziwika. Musadzizindikiritse nokha tsopano ndi Afarisi ndi iwo amene samakhulupirira, akhungu amenewo, chifukwa Yesu ananena kuti iwo sadzamuwonanso Iye. “Koma inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu. Ine ndidzakhala mwa inu. Inu mudzandiwona Ine.”

Chabwino, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo, umo ndi momwe inu mungamuwonere Iye, podzinyezimiritsa Yekha mwanjira yomweyo imene Iye ankachitira nthawi imeneyo. Kodi izo nzoona? Chabwino.

³⁰⁰ Tsopano, inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Mukhale ndi chikhulupiriro. Musakayikire, muzipemphera, ndiyeno ife ti—ifeti tiwona chimene Iye ananena. Tsopano, mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse.

³⁰¹ Tsopano, Atate Mulungu, ine ndayankhula za Inu ndi Mawu Anu. Ine ndazichita izo mwanjira yosweka, Ambuye, ine ndikudziwa, koma ndi mopambana momwe ndimadziwira. Masabata awiri onsewa, ine mowirikiza ndakhala ndi Iwo, Ambuye. Moyo wanga wonse, ine ndayesetsa kukhala ndi Iwo. Tsopano, Ambuye, lemekezani Mawu Anu usikuuno pano, pamene chitsitsimutso chikutha. Mulole izo zidziwike, Ambuye, kuti ngati ife tikuyima ndi icho chimene chiri cholondola, cholondola chidzatiyimira ife. Perekani izi, Ambuye. Kuti ife tikukhulupirira, kuti Inu munadzakhala ife, kuti mudzatenge tchimo lathu; kuti ife tikhoze kudzakhala Inu, ana a Mulungu, kuti tidzanyezimiritse Mawu a Mulungu, otsimikiziridwa, kuwapanga iwo kuwonetseredwa kupyolera mu moyo wathu wa utumiki umene Inu mwatipatsa ife. Perekani izi, Ambuye. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu tsopano mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³⁰² Tsopano mungokhala ndi chikhulupiriro. Musakayikire, koma—koma mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano. Kodi inu mukukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Aliyense akhulupirire. Tsopano, musakayikire. Mungopemphera, kwa inueni. Khalani ndi chikhulupiriro tsopano. Musakayikire, nkomwe. Dzikhazikitseni mwa bata tsopano. Mvetserani kwa chimene Mzimu ukunena kwa inu. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

³⁰³ Inu mukundiyang’ana ine moonamtima chifukwa chiyani? Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Ine sindikukudziwani inu. Ine sindinayambe ndakuwonani inu, koma mkazi chabe atakhala apo akundiyang’ana ine. Si matenda kwenikweni amene iye akuda nawo nkhwawa. Iye akudandaula za munthu winawake. Ndi mtsikana wamng’ono. Iye wangosowa kumene. Iye wachoka kwawo. Iye ndi mtsikana chabe, mtsikana wa zaka zamatini. Izi zapangidwa kwa nthawi yayitali. Mpaka pano, sindikuwona chowopsya ndi iye. Khalani ndi chikhulupiriro. Khulupirirani Mulungu, Iye amutumiza iye kunyumba kwanu.

³⁰⁴ Kodi iye anakhudza chiyani? Tsopano, inu mukumuwona mkaziyo. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga. Iye ndi, kwathunthu, mlendo.

305 Apa pali dona wakhala kumbuyo komwe *kuno*, wateka mmaso, akupemphera. Iye akuvutika ndi a—vuto la m'mimba, ndipo ndi zotupa. Iye akuvutika ndi vuto la mtima. Iye aziphonya izo. Mulungu, tithandizeni ife. Abiti Willingham, khulupirirani pa Ambuye Yesu Khristu. Tsopano inu mulandire izo.

306 Tsopano mfunzeni mkaziyo. Ndife alendo kotheratu. Inu mukuti, “Inu munatchula dzina lake.”

307 Bwanji, kodi Yesu sanamuwuze Simoni, “Dzina lako ndi Simoni. Iwe ndi mwana wa Yonasi”? Mungokhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira izo?

308 Tsopano khalani owonamtima. Khulupirirani. Musakayikire ayi. Mungoyika malingaliro anu pa Mulungu, ndipo—ndipo mumukhulupirire Iye.

309 Kodi Iye akuchita chiyani? Iye akudzizindikiritsa Yekha. Iye akudzinyezimiritsa Yekha. Tsopano, ngati inu simukuganiza kuti izo ndi zolondola, ine ndikukupemphani inu kuti mubwere ku guwa ndi kudzachita chinthu chomwecho.

310 Pali a—mkazi wamng'ono. Iye wakhala kumbuyo kuno ali ndi shawelo pamutu pake. Iye ndi wachi Spanishi. Ndipo akumupempherera mwana wamkazi. Mwana wamkaziyo samakhala kuno. Iye tsopano wayika manja ake pankhope yake. Ndipo iye ali . . . Mwana wamkazi uyu amakhala kumene kuli madzi ambiri, kumene nyanja imakukuma, ku San Diego, California. Ndipo ali ndi mitsempha yotupa ndi zovuta, ndipo watsala pang'ono kufika ku kusokonezeka kwa manjenje. Kodi iwe ukhulupirira kuti pemphero lako ndiye linakhudza mphonje ya chovala Chake, mlongo wanga wamng'ono wa Chispanishi, ndipo mwana wako wamkazi akhala bwino? Ngati iwe ukutero, kweza mmwamba dzanja lako ndipo ulandire zimenezo. Chabwino, iwe ukhoza kukhala nazo izo. Zikumveka bwino kumeneko ndi inu tsopano. Musakaikire. Khulupirirani.

311 Izo zinali zodabwitsa kwa inu, sichoncho izo, dona, wakhala pamenepo? Unakweza dzanja lako mmwamba pa mphuno yako, ndi kupukuta nkhope yako pamenepo; unanena chinachake kudutsa mu kanjira; utavala chikhoto cha buluu, wakhala pamenepo. Inde. Chabwino. Ngati iwe utakhulupirire ndi mtima wako wonse, ndiye mtima umenewo uwongoka ndipo sukhalanso ndi vuto la mtima limene iwe wakhala ukuvutika nalo. Ngati izo ziri zolondola, imirira pa mapazi ako, kuti ungochitira umboni kuti izo ndi zoono. Ndine mlendo kwa donayo. Ameni. Kodi inu mukukhulupirira? Ndithudi. Uh-huh. Khulupirirani nthawizonse.

312 Ine ndikuwona, ndipo mwamuna wa zaka zapakati kani. Kodi inu mukuwona Kuwala kumeneko, kwa ambala, kwapachikika apo pomwe, kukukokera pa munthu ameneyo? Tsopano iye akupemphera. Iye waweramitsa mutu wake pansu. Ndipo pali chinachake chimene changonedwa kumene,

chimene chinakopa chidwi chake ku kupemphera. Chifukwa, iye akuchokera ku California, nayenso, monga zanenedwa kumene. Koma iye akuchokera ku Fresno, California. Iye amadwala mphumu. Bambo Korol, ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kupita kwanu ndi kukachiritsidwa, inunso. Amen. Khulupirirani izo tsopano. Ngati izo ziri zoon, kwezani dzanja lanu. Kodi ndife alendo? Kwezani dzanja lanu. Chabwino.

³¹³ Inu mukukhulupirira? Kodi munthuyo anakhudza chiyani? Iye anamukhudza Yesu Khristu. Iye ali mapazi sarte kuchokera kwa ine.

³¹⁴ Ine ndikukubetcherani inu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti mukhulupirire kuti Uthenga uwu wa Mzimu Woyera mmasiku otsiriza ano ndi kutsekera kwa mbiriyakale ya dziko lapansi. Ndikukubetcherani inu kuti mukhulupirire kuti ine—ine ndinaphunzitsa Izo kwa inu usikuuno. Inu mukhulupirire kuti Mulungu anandituma ine. Inu mulemekeze izo. Ndipo tsopano, musandilemekeze ine, koma mulemekeze chimene Iye ananditumizira ine, Mawu Ake, ndipo Mulungu apereka icho, chopempha chanu. Ine sindingakhoze kumupanga Iye kuti achite zimenezo, koma ngati inu muti mukhulupirire.

³¹⁵ Apa, yang'anani apa. Kodi inu simukuwona Iko? Yang'anani apa, Kuwala kuja pomwe *apa*. Iko kuli pa mtundu uwu wa mkazi wonenepa kwambiri wakhala apa. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Sindinamuwonepo iye m'moyo wanga, koma iye akudwala. Iye akuvutika. Iye anapita kwa dokotala, ndipo, chinachake, kuyeza kunasonyeza kuti izo ziri mu thumbu. Izo ndi mtundu wina wa zilonda. Ayi, adokotala akunena kuti ndi zilonda za mmimba. Uko nkulondola. Uko nkulondola. Iwe si wochokera kuno. Iwe uli kuno kudzacheza. Nkulondola uko? Kweza mmwamba dzanja lako. Iwe umachokera ku Michigan. Uko nkulondola. Iwe wabwera kudzachezera mwana wako wamwamuna, ndipo ali mu mtundu wina wabizinesi ya wayilesi yamtundu wina. Dzina lako ndi Akazi a Erb. Khala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Pita kwanu ndipo ukapeze izo momwe iwe ukuzifunira izo, ngati iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse.

³¹⁶ Kodi inu mukukhulupirira? Kodi mwakonzeka kuti litsiro la kusakhulupirira lipunthidwe kuchoka mwa inu? Kodi inu mukukhulupirira kuti inu mukhoza kumuwona Khristu akudzinyezimiritsa Yekha, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Iye ndi Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Nenani, "Ameni" ngati inu mukukhulupirira izo. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi].

³¹⁷ Ndiye ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ine ndikusonyezani inu Mawu Ake, ngati inu muli okhulupirira. Iye anati, "Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira.

Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala iwo adzachiritsidwa.”
Ikani manja anu pa wina ndi mzake tsopano.

³¹⁸ Tsekani maso anu. Weramitsani mutu wanu. Muzipemphererana wina ndi mzake. Inu mupemphere. Si ine. Inu mupemphere. Khristu, kunjia pakati panu kunjia uko!

³¹⁹ Atate Akumwamba, mu Dzina la Ambuye Yesu, mulole kuti Khristu anyezimiritsidwe mu moyo uliwonse pano usikuuno. Ndipo chiritsani odwala, Ambuye. Tikutulutsa mdierekezi aliyense wa kusakhulupirira, kuti Mpingo wa pentekoste ukhoze kuwona chinyezimiro cha Yesu Khristu mmoyo wawo, monga momwe iwo awonera icho usikuuno. 🕊

63-0123 Chizindikiritso
First Assembly Of God
Phoenix, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org